


CHILEMBA CHA CHIROMBO

 Tsopano, mawa usiku. . .Ife nthawizonse tikuwonetsera chinthu chimodzi, Ambuye Yesu Khristu, ndi chokhacho, ndipo chirichonse chomwe chiri chifuniro Chake Chaumulungu kwa ife kuti tichite. Koma ngati icho chiti chikhale chifuniro Chake Chaumulungu mawa usiku, pa *Chisindikizo Cha Mulungu*, ife tikufuna kuti tiyankhulepo, ngati Ambuye alola.

² Ndipo usikuuno, ife tikupereka, ngati Iye. . . utakhale mwayi Wake kwa ife kuti tichite, kapena mwayi wathu kuti ife timuchitire Iye, kani, usikuuno, ife tikufuna kuyankhula pa limodzi la phunziro lofunika kwambiri la orali: *Chilemba cha Chirombo*.

³ Ndipo usiku watha ife tinali mu mibadwo ya mpingo, *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo*. Ndipo kuyamba ndi m'badwo wa mpingo wa Aefeso, wa Efeso; ndipo tinatsirizira pa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, m'badwo wotsiriza wa mpingo. Ndipo Ambuye atawonjezera madalitso Awo tsopano ku Mawu pamene ife tikuyankhula.

⁴ Tsopano tiyeni ife tiweramitse basi mitu yathu mwa mphindi ya pemphero, basi ife tisanati titsegule Mawu Aumulungu.

⁵ Atate Akumwamba achifundo, ife tiri oyamikira chifukwa cha mwayi uwu umene ife tiri nawo usikuuno, kukhala tiri amoyo, ndi kukhala tiri pano pa dziko lapansi, usikuuno, ndi kukhala nalo thanzi ndi mphamvu, ndi kukhoza kukhala mu nyumbayi, kumene Mawu a Mulungu akukhala ali kuwerengedwa.

⁶ Ndipo ife tikupemphera, O Muwomboli wodala, pokhala Muwomboli wathu Wapachibale Amene watitsuka ife mu Magazi Ake, ndi kutiyeretsa ife kwa tchimo, ndipo tsopano akutipereka ife kwa Atate, opanda cholakwa, mwa Khristu Yesu; mutabwera Inu, usikuuno, ndi kutenga Mawu ndi kuwatsegulira Iwo kwa mitima yathu. Mulole Mzimu Woyera uchite kuwatenga Mawu pamene Iwo ali kuphunzitsidwa, ndipo mulole Iwo apite molunjika ku malo ake, ku mtima uliwonse, mtima wanga ndi mtima wa omvera. Pamene ife tiri kuwasowa Iwo, Atate, lolani Iwo kuti aperekedwe. Ndipo mulole pasakhale wina ati ayipidwe nawo Mawu. Ndipo, Atate, ngati nthawi iliyonse imene ine ndikananena chinachake chimene chikanakhala chiri chosiyana ndi kutsogolera Kwanu, mulole Mzimu Woyera uyimitse kamwa yanga. Ine ndikukhumba kokha kuti ndidziwe chimene chiri Choonadi, ndiyeno kuti tiziyenda mmenemo.

⁷ Tidalitseni ife palimodzi tsopano, tikhulukireni ife za machimo athu, pamene ife tasonkhana mu nyumba iyi ya kupembedza. Ndipo mulole machimo athu akhale pansa pa

Magazi, ndipo mizimu yathu iyikidwe mu cholinga choyenera cha kupembedza pa nthawi iyi. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

⁸ Tsopano, ndinali kuganiza kokha, kachidutswa kakang’ono ka chipepala aka pano, ine ndinali nditalembapo Malembo angapo kuti...oti ndiziyang’anirapo, kuti tiwerenge, poti tiyambe nazo. Ndipo tsopano pamene ine ndafika pamwamba pano, izo zikuwoneka ngati ine sindikumverera kuti ndiwerenge alionse a iwo. Ndimu nthawizonse momwe izo zimayendera; zowerenga zinai kapena zisanu kuti tiyambirepo.

⁹ Koma ine ndikufuna kuti ndiwerenge kapena kunena ichi poyamba, kuti, mu kuyankhula, ine sindimachita kuganizira. Inu mukudziwa, mwinamwake, monga ngati...Ine ndiribenso zina zokonzekeredwa pa chomwe ndingati ndinene kuposa momwe inu muliri, onani, palibe kanthu. Ine ndimangoyembekezera pa Iye. Ndipo basi momwe ine ndikuziwonera izo, ine ndimangofikira ndi kuchitenga icho, ndi kuchipereka icho kunja. Ndiyeno nthawi zina izo zikhoza kumveka mwaukali pang’ono, nthawi zina, koma ziri chabe njira yokha yomwe ine ndimazilandirira izo. Chotero ndiyo—ndiyo njira yokha yomwe ine ndingakhoze kupereka izo.

¹⁰ Tsopano, mu izi, lolani izo...ine ndinene kachiwiri usikuuno. Izi siziri zolondoleredwa kwa wina payekha kapena chipembedzo cha winawake, mwaona, sichonko konse. Ife sitimakhulupirira mu zimenezo. Ife timakhulupirira kuti ife ndife Amereka enieni owona, kuti munthu aliyense akhoza kukhala nawo mwayi wa kupembedza Mulungu molingana ndi kulamulira kwa chikumbumtima chake chomwe. Ndipo ife tikufuna izo kuti nthawizonse zizikhala mwanjira imeneyo. Koma, mu mpingo uliwonse, ife tiri ndi chiphunzitso.

¹¹ Nthawi zambiri, mu mabungwe, zipembedzo, iwo ali nacho chikhulupiriro. Ndipo iwo amakhala pa chikhulupiriro chimenecho, “Ichi ndi chikhulupiriro chathu.” Ziribe kanthu zimene mlaliki aganiza, iye ayenera kuti azilalikira chiphunzitso, chifukwa iye ali mu chipembedzo.

¹² Ndipo mkati muno, ife tiribe chikhulupiriro koma Khristu, ndicho chikhulupiriro; ndipo palibe lamulo koma chikondi; palibe bukhu koma Baibulo. Ndipo Khristu ndiye Mutu; ndipo Baibulo ndilo bukhu lathu lowerenga; dziko lonse ndiye kachisi wanga. Kotero ine monga—ine ndimakonda kulalikira basi mwa njira yomwe ine ndikumverera kutsogoleredwa kuti ndilalikire, ndipo basi mwa njira yomwe ine ndikuchiwonera Icho.

¹³ Ndiyeno mu nthawi ino, poyankhula makamaka pa chowawa kwambiri ichi, cholimba, gawo locheka la Uthenga, koma, inu mukudziwa, ino ndi nyumba ya chiweruzo. “Chiweruzo chimayambira ku” (kuti?) “nyumba ya Mulungu.” Chabwino. Kuno ndi kumene chiweruzo chimayambira. Ndipo kuli...

Ngati inu mukanapita kuno koweruza milandu, ndipo inu kuti mukalandire chiweruzo, iwo ali ndi bukhu la lamulo kumeneko, iwo amayenera kuwerenga lamulo limeneli, kuti apeze chomwe iwe ukuweruziridwa nacho. Ndipo umo ndi momwe izo ziriri mu nyumba ya Mulungu, ife tiyenera kuzitenga izo kuchokera mu Mawu a Mulungu.

¹⁴ Ndipo tsopano, nthawi zambiri, mu zinthu izi, kotero kuti inu mukhale otsimikiza kuti mwachimvetsa ichi tsopano, kuti, ine ndikanakhoza kukhala ndikulakwitsa. Kutanthauzira kwanga kukanakhoza kukhala kolakwika. Koma ine ndikuyesa kuwerenga Ilo mwa pafupi basi, ndi kungonena momwe Ilo likunenera. Kungokhala molondola basi ndi Lembba, chimene Ilo likunena kuti unene.

¹⁵ Ndipo tsopano izo zangokhala zoipa kwambiri, kapena . . . Mwinamwake icho sichiri chifuniro cha Ambuye, ndipo mwina icho chiri, ine sindikudziwa, izo, ine ndikanakonda kuti ndikhale kokha ndi sabata pambuyo pa sabata mu Bukhu ili, kungokhala pomwe pomwepo ndi kuyang'ana ilo likugwirana mpaka uko mu Daniele, ndipo Daniele ndi Chivumbulutso, ndi kumangirizira mkatimo aneneri.

¹⁶ Ndipo Mawu a Mulungu onse ali pang'ono paliponse omangirizana limodzi kumene. Mabuku sikisite-sikisi, olembedwa ndi chiwerengero cha anthu, mazana a zaka motalikirana, ndipo palibe limodzi likutsutsana ndi limzake lina, palibe limodzi. Lina lirilonse la iwo mwangwirowi. Sipanapezeke konse gawo la zowerenga zomwe zinalembedwa monga Ilo, mu dziko lonse.

¹⁷ Iwo akhala, kwa zaka zikwi ziwiri, akuyesa kuti asinthe pemphero la Ambuye. Kutu ayike liwu limodzi kwa Ilo, kapena kuchotsapo limodzi pa Ilo, kuti alipange Ilo bwinoko. Inu basi simungakhoze kuchita izo. O, Ndi langwirowi. Ndi Mawu a Mulungu.

¹⁸ Ndipo ine ndikukhulupirira—Baibulo ndi Mawu a Mulungu odzozedwa. Liwu lirilonse la Ilo ndi lodzozedwa. Ine sindikukhulupirira *apa* pokha si podzozedwa, ndipo *apa* pali, ndi *apo* pali. Ine ndimakhulupirira Liri lonse lodzozedwa. Liri mwina lonse lolondola kapena lonse lolakwika; ndipo ngati Liri lonse losokonezeka, ndiye ife sitikudziwa choti nkuchita. Koma Liri, pang'ono paliponse, Choonadi. Ine ndikulolera kuti ndipereke moyo wanga pa mphindi iliyonse chifukwa cha chimene PAKUTI ÁTERO AMBUYE ali pano.

¹⁹ Tsopano, tsopano iwo akungokhala nawo mausiku angapo awa. Ndipo, pajatu, ife tidzakhala ndi msonkhano wa Loweruka usiku, kupita nazo mofanana basi, za kukhala ndi . . .

²⁰ Ena mwa anthu a mpingo anati iwo akanati . . . pokhala mwakuda, kuti abwere mu tchalitchi Lamlungu mmawa, kuti ena a iwo anati iwo akanakhala alipo Loweruka usiku,

utatha msonkhano, ndi kuthandiza kuyeretsa mu tchalitchi kotero kuti anthu asati adzabwere muno Lamlungu mmawa, kapena . . . kapena iwo sakati achite kugwira ntchito Lamlungu, kuti—kuti ayambe kukonzamo mu tchalitchi. Ife sitimati . . . Ife tikufuna . . . Ine sindine Wasabata, komabe ine ndimakonda kuti ndizilemekeza—kupembedza basi moyandikira momwe ine ndingakhazere.

²¹ Ndipo tsopano, ndiye, ine ndikuganiza ine ndidzalengeza mawa usiku, mwina ngati Ambuye alola, chomwe ife titi tidzayankhule pa Loweruka usiku.

²² Tsopano, usikuuno ndi: *Chilemba Cha Chirombo*. Ndipo mawa usiku: *Chisindikizo Cha Mulungu*. Iwo ali awiri kwambiri a . . . ine ndikuganiza, maphunziro ofunika kwambiri oti ayankhulidwepo mu tsiku lino, pakuti ine ndikukhulupirira moona kuti ife tikukhala moyo mu nthawi ya kufufuza chiweruzo ichi ya Mulungu. Ine ndikukhulupirira ife tiri kumene mu tsiku la izo. Ndipo ife sitikufuna kukhala opitiriza muyezo. Ife sitikufuna kukhala otentheka. Ife basi tikufuna kuyandikira ilo mwabwinobwino chabe monga Baibulo litayankhulire izo pano; ndipo Ndizo zangwiro, ndithudi.

²³ Ndipo tsopano mu kuchita izi, ife tikuwamva anthu ochuluka ambiri, lero, akuyankhula za chilemba cha chirombo. Inu mwamvapo izo kwa nthawi yaitali. “Ndi chiyani icho? Ndi ndani amene amachita icho? Kuti? Ndi ndani yemwe atakhale nacho icho? Ndipo ngati iwo atakhale nacho icho, chiyani—ndi chiyani chomwe icho chitachite kwa iwo? Chiyani? Chiyani? Kodi icho chingakuvulaze iwe? Kodi pali—pali choyipa chirichonse kwa icho?”

²⁴ Chabwino, tsopano, ndicho chimene ife—ife tikufuna kupeza kuchokera ku Mawu a Mulungu, chinthu choyamba, “Ngati pali chilemba cha chirombo chayankhulidwa mu Baibulo?” Ndipo chinthu chotsatira, “Ndi m’badwo uti umene icho chiti chidzakhalemo? Ndipo ndi anthu ake ati amene atadzakhale nacho icho? Ndipo iwe ungachite chiyani? Kodi iwe ungakhale nacho icho ndi nkusachidziwa icho?” Ndi zina zotero, izo, basi mafunso amenewo ngati choncho. Kotero, mwa kukhoza kwa kudziwa kwanga, kuti—kuti uwu udzakhala umodzi wa maphunziro ofunika kwambiri awiri amene ine ndingakhoze kuwaganizira mu Baibulo, *Chilemba Cha Chirombo*, ndi *Chisindikizo Cha Mulungu*.

²⁵ Tsopano, choyamba, ine ndiri ndi Lemba pano kuti ndisonyeze ngati . . . kapena kungolemba, basi kuti ine nditembenukire kwa Ilo, ndipo ilo ndi Woyera . . . Poyambirapo, tiyeni tingowona chimene chilemba cha chirombo chiri, ndi, “Kodi ndi chowopsya kukhala ndi chilemba ichi? Ndi choncho?” Tsopano mu Chivumbulutso, mutu wa 14 ndi ndime ya 9, ndi

uthenga wa mngelo wachitatu. Tsopano, wophunzira aliyense wa Baibulo . . .

²⁶ Ine ndikumuwona M'bale Stanley apa, ndi atumiki ena awiri kapena atatu akhala pano. Ndipo usiku watha apo panali abale ena pano ochokera ku Baptisti seminare mu Louisville, ndipo mwinamwake alipo ena usikuuno. Ine sindikudziwa. Ndipo alipo mwinamwake Amethodisti, Abaptisti, Akatolika, ndipo mwinamwake akhoza kukhala Myuda wa Orthodox. Ine sindikudziwa. Koma sindizo ayi . . .

²⁷ Izi sikuti ndipweteke kumverera kwa aliyense; osati konse. Ndipo ndizo chabe za . . . Basi momwe Baibulo lalembedwera, kuti tiwerenge Ilo, ndi kulola inu kuyang'ana pa Ilo, inueni. Ndipo tiyeni tiyandikire Ilo basi mwabwinobwino monga ife tikudziwira, mwa kuwopa Mulungu, podziwa kuti Iye adzatiweruza ife chifukwa cha mawu athu. Mawu athu mwina adzataliditsa ife kapena adzatitsutsa ife pa Tsiku la Chiweruzo.

²⁸ Ndipo ngati ine ndikumverera kuti ine ndikudziwa chinachake, ndipo nkuchisunga icho, ndiye Mulungu akandipanga ine kulipira kwa icho pa Tsiku la Chiweruzo; ndipo miyoyo ndi manja awo, zikunena, "M'bale Branham, ngati inu mukanangotiuza ife, ife sibwezi tiri mu chikhalidwe ichi lero."

²⁹ Ine ndikufuna kuima ngati Paulo wa kale, "Ine ndine mfulu kwa magari a anthu onse. Pakuti ine sindinaleke kunena kwa inu uphungu wonse wa Mulungu." Ndiko kulondola, basi monga ine ndikuwona Iwo; ndipo ngati ine ndikulakwitsa, ndiye Mulungu andikhululukire ine. Zinthu izi sizibwera konse . . . Ine sindinapite ku seminare iliyonse, sindinapite konse ku sukulu iliyonse, ine sindinatenge konse mawu a aliyense za Izo. Ine ndinapita molunjika kumene kulowa mu Baibulo, mwa pemphero. Ndipo izi ndi zowululidwa Mwaumulungu ndi Mzimu Woyera, Mngelo yemweyo wa Mulungu amene amandilondolera ine kuti ndiziwona masomphenya ndi zina zotero monga chomwecho, ndi kuchiritisa kwa odwala. Ndipo inu mukhoza kuweruza mwa zimenezo ngati Izo zingakhale zolondola kapena ayi.

³⁰ Tsopano, uwu ndi uthenga wa mngelo wachitatu, kwa dziko. Ndipo inu mukudziwa chiyani, uthenga wa mngelo wachitatu, iwo uli nkupita tsopano mu tsiku ili. Uku ndi kuwuluka kwa uthenga wa mngelo-wachitatu, ngati ndinu wowerenga Baibulo.

³¹ Apo panali matsoka atatu anatsatira iwo. Loyamba limodzi linachitika mu Nkhondo ya Dziko lonse Yoyamba. Lina Lachiwiri linachitika mu Nkhondo ya Dziko lonse Yachiwiri. Inu mukuona chimene ife tikulowamo tsopano. Chabwino. Ife tiri pa mapeto a msewu.

³² Tsopano tiyeni titengere izi pa malingaliro athu, basi ife tisanawerenge Lembu. Mwapamalo, ife tiri pakuti tikhale pa

m'badwo wotsiriza. Motalika bwanji? Ine sindikudziwa; palibe mmodzi angathe.

³³ Koma, penyani, tiyeni titenge kuyankhula mwambiriyakale. Zaka zikwi ziwiri zoyamba, dongosolo la dziko linafika pachimake, ndipo Mulungu analiwononga dziko ndi madzi. Inu mukudziwa zimenezo? [Osonkhana anena, "Ameni."—Mkonzi.] Ndiye ilo linatulukira ngati dziko latsopano. Ndipo zaka zikwi ziwiri zachiwiri, ilo linafika kumapeto ake kachiwiri, ndipo Mulungu anamutuma Yesu. Kodi nkulondola uko? ["Ameni."] Awa ndi mapeto a zaka zikwi ziwiri zotsatira, 1954. "Ndipo Uthenga," Yesu anati, "ntchito idzadulidwa mofupika," (kwa chiyani?) "chifukwa cha osankhidwa, kapena panalibe mnofu umene ukanapululumutsidwa," iwo udzayipa kwambiri. Kotero ife tiri pa mapeto a nthawi. Ndiyeno wachisanu ndi chiwiri, mu kuyimira, ndi Zakachikwi, zaka chikwi.

³⁴ Monga Mulungu anavutikira zaka zikwi zisanu ndi chimodzi, ife tikudziwa kuti zaka chikwi... "Tsiku limodzi Kumwamba ndi zaka chikwi pa dziko lapansi," Petro Wachiwiri. Mwaona? Tsopano, ndipo Mulungu anamanga dziko mu zaka zikwi zisanu ndi chimodzi. Ndipo Mpingo unavutikira motsutsa tchimo tsopano kwa zaka zikwi zisanu ndi chimodzi. Ndipo chikwi chachisanu ndi chiwiri, Mulungu anapita kukapumula, ndipo anapumula chachisanu ndi chiwiri; ndipo, tsopano, choyimira cha Zakachikwi, Mpingo Kuti ukhale pa dziko lapansi pano, pomwe pano mu mawonekedwe a thupi, kwa zaka chikwi, opanda kudwala, zodandaulitsa, zovuta, kapena imfa. M'badwo wopambana, wagolide uwo ukubweramo tsopano! O, pa zimenezo! O, ine ndimakonda nyimbo imeneyo:

Dziko likubuula, kulirira tsiku la kumasuka
kokoma,
Pamene Yesu ati adzabwererenso ku dziko
lapansi. (Ine ndimaikonda imeneyo.)
Tchimo ndi zodandaulitsa, zowawa ndi imfa za
dziko la mdima ili zidzatha,
Mu kulamulira kwaulemerero ndi Yesu kwa
zaka chikwi kwa mtendere.

Baibulo linati, "Iwo analamulira ndipo anakhala mu mpando ndi Khristu zaka chikwi", Mileniyamu.

Tsopano, uthenga wa mngelo wachitatu uwu, Kudza kwa Ambuye kusanachitike kumene, pamene chisindikizo ndi chilemba chinali kuyikidwapo. Tsopano kudzakhala kuli kukusa kwakukulu, kukusa.

³⁵ Uko Kumadzulo, pamene ife tipita kunja, ine ndinkakonda kutero, ine ndakhala kuyambira ine ndiri mnyamata, kupita kunja ku kukusa kwa Mchirimwe ndi kukusa kwa Mdzinja, kupita mmaphiri ndi kuthamangitsira ng'ombe kumusi. Ndipo ife tikatha kuzipeza ng'ombe zonse ife timakhoza kuzipeza,

kuchokera ku malo aliwonse, ndiye ife timadula zonse zamu . . . zimene siziri za ife. Zathu zinali ndi chizindikiro, ndipo izo zimaikidwa chizindikiro. Ndipo ngati inu mukanati . . .

³⁶ Kodi aliyense anayamba wazonapo ng'ombe zoikidwa chizindikiro? Ndi chinthu ndithu kuwawonera iwo akuika chizindikiro ng'ombe. Ine ndinkakhala ndikuzimvera chisoni ng'ombe. Ndipo ndi nyansi kwambiri zodwalitsa pamene iwe uyamba kuziyika chizindikiro ng'ombe. Kuwotcha chitsulo choyikira chizindikiro inali kukhala ntchito yanga, kunyamula chitsulochi. Ndi kuchiyika icho pa ng'ombe yaying'ono itagona pamene, ndi mapazi ake atamangidwa; ndi kuika chizindikiro chimenecho pa iyo, ndipo ubweya ndi nyama zikuwotcheka; kuponyera tara pang'ono pa iyo, ndi kumumasula iye. Ndipo kuyankhula za kupita! Iyo imapita kwenikweni. Koma, yang'anani, iyo yayikidwa chizindikiro.

³⁷ Ndipo umo ndi momwe Mulungu amatichitira ife. Iwe uyenera kufika pansu ku guwa ndi kumangidwa ngati nkhumba, kamodzi mu nthawi. Koma, m'bale, pamene Mzimu Woyera uyika konse chizindikiro pa iwe, iwe ukhoza kuchitapo kuthamanga kwina ndi kukuwa, koma iwe waikidwa chizindikiro. Ndiko kulondola. Iwe uli pamene. Pamene Bwana abwera, Iye akudziwa kuti ndiwe wakuti.

Koma, o, kwa yosochera ya chaka chimodzi iyo, munthu uyo amene watsutsidwa kuti amasulidwire mkati pa—akumidzi.

³⁸ Tsopano, nthawi yoyika chizindikiro. Ndipo tsopano pakhala okwera awiri okha mu izi, ameneyo akhala Mulungu ndi Satana. Satana atenga ake, ndipo Mulungu atenga Ake. Usikuuno ife tiwona amene akuvala chizindikiro cha Satana, ndipo mawa usiku ife tiwona yemwe akuvala chizindikiro cha Mulungu, molingana ndi Mawu a Mulungu.

³⁹ Tsopano pano pali uthenga wa mngelo, ndime ya 9 ya mutu wa 14. Tiwerenge Malemba angapo awa pano, amene ine ndawalemba. “Ndipo mngelo . . .”

Ndipo mngelo wachitatu anawatsata iwo, akunena ndi liwu lalikuru, Ngati munthu aliyense alambira chirombo, ndi fano lache, nalandira lemba lake mu mphumi yake, kapena . . . dzanja,

Omwevo adzamwako za vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, umene ukutsanuliridwa popanda kusakaniza mu chikho cha mkwiyo wake; ndipo . . . adzazunzidwa ndi moto ndi miyala ya sulfure pamaso pa angelo oyera, ndi pamaso pa Mwanawankhosa:

⁴⁰ Zedi sindikufuna kanthu kochita ndi zimenezo! Penyani.

Ndipo utsi wa kuzunzika kwao unakwera mmwamba kwa nthawi za nthawi: ndipo iwo alibe mpumulo usana kapena usiku, amene apembedza chirombo ndi fano

lake, ndi aliyense amene alandira chilemba cha dzina lake.

41 Ine sindikufuna kanthu kochita ndi zimenezo, ine ndiri wotsimikiza. Eya. Mvetserani ku ndime yotsatira, pamene ine ndikuyang'ana pa iyo.

Pano pali chipiriro cha oyera: pano pali iwo amene asunga malamulo a Mulungu, ndipo ali ndi chikhulupiriro cha Yesu Khristu.

42 Tsopano mutu wa 15, ndi ndime ya 2. Ndipo. . . Mvetserani tsopano, mu mutu wa 15 ndi ndime ya 2. Tsopano, ife tinali kuwerenga ndiye kuchokera ya 14, ndi ndime ya 9. Tsopano wa 15, ndipo ndime ya 2.

Ndipo woyamba anapita, natsanulira mbale yake pa dziko lapansi; ndipo pamenepo panagwa pokhoso. . . zironda zoipa pa. . . amuna amene anali ndi chilemba cha chirombo, ndi pa iwo amene apembedza fano lake.

Mutu wa 16 ndipo ndime ya 2.

Ndipo ndi amene mafumu a dziko lapansi anachita naye chiwerewere, ndipo okhala padziko lapansi alidzeretsedwa ndi vinyo wa mkwiyo wa chiwerewere.

43 Miniti chabe. Ine ndikupempha kukhulukira kwanu. Ine ndinatembenuza, ndiyenera kuti ndinatembenuza awiri a iwo kamodzi. Chabwino. Tsopano mutu wa 20 ndi ndime ya 4. Chabwino, apa ife tiri.

Ndipo ine ndinaona mipandoyachifumu, ndi iwo amene anakhala pa iyo, ndipo chiweruzo chinaperekedwa kwa iwo: ndipo ine ndinaona miyoyo ya iwo amene anadulidwa mitu chifukwa cha umboni wa Yesu Khristu, ndi chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi amene sanalambire chirombo, kapena fano lache, kapena sanalandire chilembacho pa mphumi zawo, kapena mu dzanja lao; ndipo iwo anakhala moyo ndipo analamulira ndi Khristu zaka chikwi.

44 Sungakhoze kulandira chilemba cha chirombo ndiyeno nkupembedza Khristu kapena kukhala ndi Iye. “Koma aliyense amene ati adzapembedze chirombo kapena fano la chirombo, adzazunzidwa mu kukhalapo kwa Mulungu ndi mu kukhalapo kwa angelo oyera.” Ndicho chimene Ambuye amanena za icho.

45 Tsopano ife tati tiyambe. Tembenuzani mu Baibulo lanu tsopano ku mutu wa 13 wa Chivumbulutso, ndipo ife tiyamba mu mphindi pang'ono chabe. Tsopano izi ndi zofunika kwambiri. Ndipo mvetserani mwatcheru tsopano.

46 Poyamba, ife tikufuna kutenga phunziro lathu kuchokera pa usiku watha. Usiku watha ife tinatenga pa mibadwo ya mpingo, kuti, momwe ife tinawonera Yesu akuima mu Mpingo Wake,

“Akuyankhula ngati liwu la madzi ambiri; ndipo Iye anali ndi tsitsi ngati ubweya; maso ngati malawi a moto.”

47 Kumbukirani, onse—Vumbulutso liri masomphenya, ndipo mwachiphiphiritso. Zonse za izo ziri ndi tanthauzo, kotero inu muyenera kupenya mwatcheru. Kuwawerenga aneneri, kuwona chimene ziphiphiritso zinkatanthauza, ndiye nkufanizitsira izo cha kuno kotero kuti inu mudzadziwe chimene zophiphiritsazo zimatanthauza kwenikweni.

48 “Anali ndi maso ngati malawi a moto,” akuthamangira uku ndi uko kupyola pa dziko lapansi. Ndipo ife tinapeza kuti malawi amenewo, monga...“Malupanga, lupanga linatuluka kuchokera mkamwa Mwake, ndipo lupanga-lakuthwa konsekonse,” ndipo ife tinapeza kuti amenewo anali Mawu a Mulungu amene anapita kuchokera mkamwa mwa Mpingo. “Ndipo Ilo likanakhoza kudula ngakhale mpaka ku mafuta a fupa, ndi ozindikira malingaliro ndi zamkati mwa mtima,” Ahebri mutu wa 4.

49 Ife tinaupeza Mpingo utayima pamenepo mu kukongola Kwake; Khristu atawumbidwa kumene mwa Iwo! Ndipo Mpingo unali utavala “chovala” choyera. Ndipo inu munazindikira, Iwo unali mkazi, “kuzungulira pa chifuwa,” Iwo unali ndi chovala chophimba pa manyazi Ake; ndipo unali ndi “chingwe cha golide” chokokedwera mozungulira icho, chimene chinagwirizitsira iwo pozungulira pa chifuwa. “Choyera,” kunena za chilungamo cha Khristu; ndipo “chingwe cha golide” chimaimira Uthenga. Kulalikira kwa Uthenga kumabweretsa Mzimu Woyera pa Mpingo, chilungamo cha Khristu; chimaugwira iwo pamenepo, utamangidwa ndi chingwe, chingwe chomangira.

50 Ndiye Iye anali kuima pa, “mapazi ngati mkuwa, umene unali utawotchedwa mu ng’ango.” Mkuwa umayankhula za chiweruzo Chaumulungu. Ndipo Mulungu, kuti akondweretse lumbiriro Lake lalikulu limene Iye anatenga, Iye anatumiza Khristu, ndipo Khristu analipira chiweruzo Chaumulungu. Ndiyeno Mpingo wakhazikitsidwa pa chiweruzo Chaumulungu, Khristu akuima mu malo Ake. Ndi chithunzi chokongola bwanji, “Akuima mu Zoikaponyali Zisanu ndi ziwiri za Golide!”

51 Ndiyeno ife tikupeza kuti, m’badwo wa mpingo woyamba, chimene iwo anali nacho. Ndi angati anali pano usiku watha, ine ndikuwona dzanja lanu? Chabwino, ndizo zabwino. M’badwo wa mpingo woyamba, ife tikupeza, mu M’badwo wa Mpingo wa Efeso, iwo anali ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo iwo ankawabatiza anthu mu madzi, ndipo iwo anali... Mitundu yonse ya zizindikiro ndi zodabwitsa zinali zoti ziwatsatire okhulupirira.

52 Ndi momwe, mu m’badwo wa mpingo uliwonse, Iwo unayamba kuzimirira. Kuzungulira kwachiwiri, kuzungulira

kwachitatu, ndiye kupyola m'badwo wa mdima. Ndipo iwo anatulukamo ndi dzina labodza, ndi ubatizo wabodza, wonse wa madzi ndi Mzimu Woyera.

⁵³ Ndiyeno iwo anafika mpaka pansu, m'badwo wotsatira, ndipo iwo anawalitsidwapo pang'ono. Ndiyeno apo panali khomo litaikidwa, kwa kutsegula, pakati pa M'badwo wa Mpingo wa Filadefia ndi Laodikaya.

⁵⁴ Ndiyeno Laodikaya anafika pofunda ndipo anapita kunja kwa Iwo wonse, mpaka Mulungu anawulavula iwo kuchoka mkamwa Mwake. Ndiko kulondola. Ndilo Lemba.

⁵⁵ Ndipo wazambiriyakale aliyense ndi wokhulupirira aliyense wa orthodox amadziwa kuti Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo iyo, kapena “Zoyikaponyali Zisanu ndi ziwiri za Golide,” monga Baibulo linanena, zinali Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo. Monga zoyimira za Chipangano Chakale mu Chatsopano kuno, ndipo basi monga izo zimatuluka kunja.

⁵⁶ Koma apo ndi poti pakhala kugwedeza kwakukulu ndi chitsitsimutso basi kusanafike kutseka kwa nyengo ya Amitundu, Ayuda asanawutengenso Iwo.

⁵⁷ Kumbukirani, Amitundu ali kokha ndi kuchuluka kwa nthawi yowerengeka, ya chisomo. Baibulo linati, “Iwo akanapondereza pansu makoma a Yerusalemu,” Yesu anati, “mpaka nyengo ya Amitundu idzakhala itatsirizidwa.” Ndiko kulondola. Iwo uli ndi nthawi yotsimikizika yokhazikidwa yothera.

⁵⁸ Ndipo ife tikupezapo zinthu zimene iwo anachita kumbuyo uko. Ife tikuzindikira zizindikiro ndi zodabwitsa zimene zinkawatsata iwo, momwe Khristu anawauzira iwo momwe izo zinaliri zodabwitsa, ndi momwe iwo analiri. Ndiye Kuwala kunayamba kuzirala ndi kuzirala, kunatuluka kunja. Ndiyeno basi pa kutseka, uko kukanakhala khomo lina lotseguka loyikidwa kwa Mpingo. Tsopano tiyeni tiime pomwe pano ife tisanalowe mu izo. Zindikirani, tiyeni titenge uneneri wina umene ukubwera pa maganizo anga. Mneneri anati, “Apo padzakhala tsiku limene sipadzakhala konse usiku kapena masana.”

⁵⁹ Kodi ine ndikufuula kwambiri? [Osonkhana anena, “Ayi.”—Mkonzi.] Ngati inu mungathe, inu mukhoza kuchuna chimenecho pang'ono. . . Ine ndikudziwa icho chikupokosera, ndipo ndicho chifukwa ine ndikuyankhula mokweza pang'ono, kotero anthu amene ali mmbuyo akhale otsimikiza kumvetsera izo. Chifukwa, Izi ndi zofunika kwambiri.

⁶⁰ “Ndipo padzakhala nthawi, tsiku,” mneneri anati, “limene silidzakhala konse usiku kapena masana.” Mwa kuyankhula kwina, iko kudzakhala kuwala, koma ilo lidzakhala la mitambo, onani, tsiku lamitambo. “Koma mu nthawi ya usiku kudzakhala Kuwala.” Ndi chithunzi chokongola bwanji!

⁶¹ Tsopano, pamene m’bandakucha utulukira pa tsiku lamitambo ili, izo zikutanthauza kuti apo padzakhala nkondo, ndi mavuto, ndi zokwera-ndi-zotsika, ndi nyengo, ndi mipingo, ndi timalingaliro, ndi chirichonse. Iko sikudzakhala kuwala ngakhale mdima. Iyo idzakhala nthawi imene ife tidzadziwe kuti pali Mulungu, ndipo pali Uthenga, koma iwo basi mophweka sangakhoze kupenya kupyola Iwo. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza? Iwo adzati, “Baibulo linanena kuti iwo anachita *izo* kumbuyo uko pa Pentekoste, iwo anachita *izo* mu Mpingo woyambirira, iwo anali ndi zizindikiro izi ndi zodabwitsa, koma wathu—wathu mpingo wathu sumaphunzitsa Izo.” Mwaona, ndiwo mtambo, osati mdima kapena usana. “Koma, komabe, ife timakhulupirira mwa Yesu Khristu. Ife tikukhulupirira mu Kudza Kwake kwachiwiri, ndipo ife tikudziwa kuti Iye akudza.”

⁶² Baibulo linati, “Iko sikudzakhala kuwala ngakhale mdima.” Iwe sungakhoze kulitcha ilo tsiku, ndipo iwe sungakhoze kulitcha ilo usiku. Koma, zindikirani, “Mu nthawi yamadzulo kudzakhala Kuwala,” mu nthawi yamadzulo!

⁶³ Pamene anthu akummawa... Bukhu ili ndi Bukhu la kummawa; Baibulo liri. Pamene Kuwala poyamba kunatulukira pa Mpingo woyambirira, ku Efeso, chabwino, ife tikukumbukira ndi kuwona chimene chinachitika kumeneko; Kuwala kwa Mulungu kunabweretsa kupyolera mwa Yesu Khristu, mwa kutsanulira koyamba kwa Mzimu Woyera. Iko kunapereka Kuwala kwa dziko lonse, ndipo kunalemba Baibulo. Kodi ndi kulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁶⁴ Tsopano Iye analonjeza, pa dziko lakumadzulo, dzuwa limatuluka kummawa, pa kuyamba kwa nyengo ya chisomo, ndipo tsopano dzuwa likulowa kumadzulo, pa anthu akumadzulo. Ife ndi anthu akumadzulo. [M’bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ndipo Iye analonjeza kuti kudzakhala chitsitsimutso ndipo kudzakhala Kuwala mu nthawi yamadzulo. Tiri pano. Kuwala kukuwala, “ndipo mdima sunakuzindikire Iko ayi.” Ndi zimenezo. “Anthu amakonda ntchito zoyipa bwinoko kuposa momwe iwo amachitira ntchito zabwino.”

⁶⁵ Koma ilo pamene likukonzekera kugwera pa mzere wakutali. Ndipo ndi Kuwala kocheha bwanji kumene ife tiri nako, gwiritsitsani kwa Iko. Penyani, Ndi dzuwa lomwelo limene linatuluka kutsidya pa Ayuda, likulowa pano pa Amitundu. Onse kupyola mu m’badwo pano, kupyola zaka mazana awiri izi, iwo anali ndi *izi*, ndi *izo*, ndi mabungwe ndi nyengo, ndi *izi* ndi *izo*. Ndipo anthu sakudziwa pamene iwo akuima.

⁶⁶ Koma Baibulo likulonjeza, Mulungu anatero, kupyolera mwa aneneri, kuti, “Mu nthawi yamadzulo kudzakhala Kuwala.” Iko kudzakhala Kuwala mu nthawi yamadzulo. Ine

ndikukhulupirira ife tiri pano. Dzuwa likulowa. Chirengedwe chonse chikubuula, kulirira tsiku limenelo. Zindikirani.

⁶⁷ Tsopano ife tikupeza, kuti, chimene iwo anali nacho uko pa m’badwo woyamba kumene wa mpingo, iwo anatenga chiphunzitso chachirendo. Chinthu choyamba, icho chinangokhala “ntchito zina.” Iye anati, “Iwe ukudana nazo ntchito za Anikolai.”

⁶⁸ Ine ndikudabwa chimene Chinikolai chinali? Ine ndinafufuza zimenezo mopyola, ndi kupyola mbiriyakale, mobwereza ndi kubwereza ndi kubwereza, kupyola ndemanga zabwino kwambiri ine ndikanakhoza kuzipeza, ndipo palibe aliyense akanakhoza kudziwa, kupatula ngati icho chinali chiphunzitso chimene chinayambitsidwa ndi munthu, Nik, Nikolasi, amene anali kuganiziridwa kukhala mmodzi wa atumwi amene anakhala ngati anapita mosochera. Iye anadziyikira chikhulupiriro, kapena chinachake chimzake, ndipo kuchokera pamenepo kunayambika Chinikolai. Izo zinali ntchito, poyamba. Ndipo zimene zinali “ntchito” mu Efeso, mu m’badwo wa mpingo wotsatira zinadzakhala “chiphunzitso.” Ndiyeno chinapita mu mibadwo ya mdima ya kuzunza.

⁶⁹ Tsopano chiphunzitso chomwecho cha Chinikolai chimene chinayambika apa mu mpingo woyamba, kutatha kuzungulira koyamba kutatu kapena kunai kwa atumwi icho chinadzakhala ntchito. Iwo anayamba kuganiza, “Chabwino, *ichi* chingakhale chiri Icho.” Tsopano nonse a inu mukudziwa momwe izo zatulukira, ndi inu owerenga Baibulo.

⁷⁰ Tsopano, izo zinayambira pafupi a.d. 600 ndi . . . kapena 306, chimene iwo amachitcha kutembenuka kwa Konstantini. Iye sanatembenuke nkomwe. Mwamuna amene angachite zinthu zauve zimene munthu uyo anachita, sanali atatembenuzidwa. Ndiko kulondola. Chinthu chokha chimene iye anachita konse, chimene chinali ndi chirichonse—chachipembedzo chirichonse kwa icho nkomwe, iye anaika mtanda pa tchalitchi cha Sofia Woyera. Kodi icho sichinali chinachake, choti upitire nacho Kumwamba? Chabwino. Iye anawauza Akhristu, ngati iye akanati akapambane nkondo imeneyo, iye akanakhala Mkhristu. Ndipo iwo anapemphera. Ndipo iye anapita uko ndipo anapambana nkondoyo, kapena kupambana kumenyanako, ndipo iye anabwerako ndipo anati, “Chabwino, ine ndijowina mpingo.” Choyimira chokongola kwambiri cha mamembala wofunda wa mpingo lero. Ndiko kulondola. Kuika mtanda pa tchalitchi.

⁷¹ Itachitika imfa yake . . . Iye anali ndi ana aamuna awiri, ana aamuna atatu; Konstantini, Konstantiasi, ndi Konstantinopo, amene anayambitsa kupanga kummawa ndi kumadzulo kwa Roma, ndipo iwo anagawikana. Ndipo mmenemo, ndiye, munakhala Ufumu wa Ottoman, motsatira mu nthawi imeneyo.

⁷² Ndiyeno, iwo, pafupi kuzungulira kwachiwiri, kapena kwachitatu, kuzungulira kwachinai kwa atumwi; ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anayamba kukangana pakati pa wina ndi mzake. Ndipo iwo anagawikana, kalingaliro kakang'ono.

⁷³ Aliyense, inu muwutenge mpingo... Uko, pamene mpingo wa Chiwesile wa Methodisti uja unali mu mphamvu, iwo unali mphamvu pamene Joni Wesile anali kuno. Wa Lutera unali, mu tsiku lake; ndi wina uliwonse. Koma mulole woyambitsayo afe, kamodzi, ndiyeno iwo amapita mosochera.

⁷⁴ Pamene Ambuye anawonekera koyamba mmbuyo kutaliko; pamene iwo ankafuna ine kuti ndiyambe, kupanga bungwe pa Izi, zotero monga chonchi. Ine ndinapita uko, ndipo ine ndinaona kumene Dwight Moody, woyambitsa wamkulu, Sukulu ya Baibulo ya Moody. Ndipo ine ndinaganiza, “Ngati Dwight Moody angakhoze kuyang'ana pa Sukulu ya Baibulo iyi; chimene munthu uyo anaima nacho, ndi chimene iwo akuchita tsopano!”

⁷⁵ Chabwino, ine ndinati, “Penyani kuno, penyani, bwanji ngati—bwanji ngati Wesile, Kalvin, Knox, Sankey, kapena Finney, aliyense wa iwo, akanawuka lero, ndi kuwuona mpingo wawo kumene uli!” O, mai! Onani, kuzungulira koyamba, pamene munthu ali kuima pamenepo, iye amagwirira Choonadi.

⁷⁶ Yang'anani pa Dr. Dowie mu Mzinda wa Zioni, bwanji, lero, kuseka kumene mu nkhope ya machiritso Auzimu, pamene—mzinda unakhazikitsidwira pa iwo. Koma pamene Dowie anafa, ndiye panatulukira chiyani... Blake, John Lake ndi onse amenewo. Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo watsirizikira mozungulira tsopano mpaka a Assemblies of God alowa mu izo, ndi gulu lalikulu la zamaonekedwe ndi chirichonse. Ndipo—mpingo wapita ndi kubwerera mmbuyo, ndi mu chikhalidwe chonyansa.

⁷⁷ Kotero ine ndinapeza izi, Baibulo linati, “Davide anawatumikira Ambuye bwino mu m'badwo wake.”

⁷⁸ Kotero ine ndinati, “Ambuye, ine sindikufuna bungwe. Ndiroleni ine ndikutumikireni Inu ndi mtima wanga wonse, pamene ine ndiri pano wamoyo.” Ndiko kulondola. “Chotsatira, Inu mudzakhala naye munthu wina pamene ine ndiri nditachoka. Inu mudzakhala naye winawake kutenga malo ake. Ndizo zonse.

⁷⁹ Musati muyesere kumanga pa wina wake. Inu sumungakhoze kupanga moto pa malo omwewo. Israeli amayenera kumapitirira kumayenda. Pamene iwo amaima, iwo amabwerera mmbuyo. Iwo amayenera kupitirira kuyenda usiku uliwonse; kupanga moto watsopano usiku uliwonse; kumangopitirira kupita patsogolo. Ndipo ndicho chimene ife tiyenera kuchita. Chimene Lutera anali nacho chinali chabwino; icho chinali cha tsiku la Lutera. Chimene Wesley anali nacho chinali chabwino; ilo linali

tsiku la Wesile. Chimene achiyero anali nacho, icho chinali chabwino; icho chinali cha tsiku lawo. Ife tikukhala mu tsiku lina. Tsopano ife tiri—ife tikupita patsogolo. Ndipo padzakhala tsiku tikapita ife, ilo lidzabwera mofanana basi. Koma tiyeni tiziyenda mu Kuwala pamene Kuwala kuli pano tsopano.

⁸⁰ Ndipo ine ndikuzindikira ichi, kuti, mmenemo chiphunzitso ichi chikukhala, chinthu choyamba inu mukudziwa, mpaka icho chinaswekera mu gulu la timalingaliro, ndiye Aroma anatembenezidwa. Tsopano, ufumu wa Chiroma, kuyambira masiku a—a Roma kulanda koyamba ndi kupambana nk'hondo ya Amitundu pa Greece, kutachitika kugwa kwa Alexander the Great, lakhala liri fuko lolamulira la m'dziko; anthu Achiroma, m'badwo wa Amitundu. Daniele ananena choncho, mu masomphenya. Ife tifika ku zimenezo, mu—mu maminiti pang'ono. Koma ilo nthawizonse lakhala ndi mphamvu zolamulira pa dziko lonse; Chiroma.

⁸¹ Ndiyeno ife tikupeza kunja uko, ndiye, kuti iwo anaupanga bungwe mpingo. Gulu la anthu linakhala pamodzi, pafupi 606, ndi kudziticha okha, “makolo oyambirira,” makolo a mpingo. Magulu a amuna anadza pamodzi ndi kuchititsa khonsolo ya chimene iwo ayenera kuchita, ndipo iwo anakhazikitsa bungwe.

⁸² Ndipo mudirole ine ndiyankhule pano, abwenzi anga okonedwa a Chikhristu, onse Achiprotestanti ndi Achikatolika. Ndipo tsopano, ine ndikuganiza ine ndiri nawo abwenzi Achikatolika amene akhala pano; ine sindikunena izi kuti ndipweteke kumverera kwanu. Chifukwa, ingodikirani maminiti pang'ono chabe, ndipo ife titengera Branham Tabernacle mmenemo nayenso, onani, miniti chabe. Ife tiyenera kokha kulalikirira Uthenga monga Iwo waikidwira pano. [M'bale Branham agogoda pa guwa kasanu—Mkonzi.] Ziribe kanthu kumene. . . Yohane anati, “Nkhwangwa inali itaikidwa ku muzu wa mtengo,” siyani zibanthu ziziulukira kulikonse kumene izo zikufuna kutero. Ndiko kulondola. Iye ayenera kudula mitengo ndi zinthu.

⁸³ Koma, penyani, mkati mmenemo iwo anapanga bungwe mpingo woyamba. Ndipo iwo anakhala pamodzi ndi kupanga bungwe mpingo woyamba, umene unkatchedwa mpingo wa konsekonse, kapena mpingo wa Katolika mu Roma. Ndipo Akatolika amanena kuti iwo ndiwo “mayi wa mpingo.” Ndipo ndizo chimodzimodzi zooni. Ndiwo manthu mpingo wa chibungwe. Mokhoza. Ndi nthawi woyamba, mu mbiriyakale ya dziko lonse, imene nkale lonse panakhala pali mpingo wopangidwa bungwe; panalibe konse, kuchokera ku m'bandakucha wa nthawi.

⁸⁴ Kupyola mu masiku a Israeli, iwo sanali ayi—iwo sanali bungwe. Iwo anali mtundu, osati bungwe. Ndipo iwo. . . Yesu Khristu sanapange bungwe mpingo nk'omwe. Palibe wa atumwi

anapanga bungwe mpingo. Ndipo palibe nthawi kupyola, itatha mibadwo itatu kapena inayi atachoka iwo, anapangapo konse bungwe mpingo. Ine ndikufuna kuti inu mubweretse mbiriyakale ndi kuika chala chanu pa... Mundiwonetse ine pamene izo ziri. Ndipo ine ndawerenga Josephus ndi onse azambiriyakale odziwika kwambiri amene ife tiri nawo mdziko lero, amene ine ndikuwadziwa, chifukwa ine ndiyenera kukhala wotsimikiza. Ine ndikupanga kuyankhula uku pamaso pa zikwi za anthu; iwe uyenera kukhala wokhoza kudziteteza ndi kutsimikizira chimene iwe ukuyankhulapo. Ndiko kulondola. Uko kunalibe konse bungwe. Ndipo osati...

⁸⁵ Ndipo Petro Woyera sanayambitse konse mpingo wa Katolika. Ine ndikufuna mbiriyakale imodzi, kapena chidutswa chimodzi cha Lemba. Petro Woyera anali mwamuna wokwatira. Inu mukuti iye anali papa. Iye sakanakhoza kukhala papa. Petro anali mwamuna wokwatira. Baibulo linati, “Mpongozi wake wamkazi anagona chidwalire ndi—ndi malungo, ndipo Yesu anamuchiza iye.” Ndipo monga ine ndikudziwira, Petro Woyera sanapite konse mu Roma. Ndipo palibe mbiriyakale imene imasonyeza konse kuti iye anali mu Roma. Ndipo ndiko kulakwitsa.

⁸⁶ Koma iwo anapanga bungwe ndipo anakhazikitsa limodzi mpingo wotchedwa mpingo wa konsekonse. Kumeneko iwo anapanga pemphero la konsekonse. Iwo anali ndi chiyanjano changwirowo; aliyense amayenera kukhala limodzi, aliyense akunena chinthu chomwecho. Pemphero lomwelo limanenedwa.

⁸⁷ Ndipo iwo anapanga mulu wa Lemba, kuwatenga iwo kuchokera mu Baibulo, ochuluka a iwo, ndi kuwapanga ena. Palibe ayi purigatorio amene anatchulidwa nthawi imodzi mu Mabuku onse opatulika a Baibulo; mulibe “tikuoneni Maria,” mulibe kanthu konga zimenezo. Ziri nthawizonse zosiyana, motsutsa izo, paliponse mu Lemba. Munalibe konse izo, pa nthawi iliyonse. Ndipo ngati inu mungapeze malo aliwonse, inu muli nawo mwayi wobwera mawa usiku ndi kundikonza ine. Mulibe mmenemo, paliponse; kabweretseni ansembe anu kapena abusa. Mulibe malo, mu Lemba, amene izo zikutchulidwa konse.

⁸⁸ Bukhu lokha laling’ono, la Maccabees, limene linawonjezedwa mwa Ili, limene siliri lowuziridwa; zinthu zimene zinaikidwa mwa Ili, kapena kuchotsedwa mwa Ili. Baibulo *ili* liri Limodzi lokhalo. Ndi...Ndi zozindikiridwa ndi oyambitsa oyambirira, kapena aliwonse a azambiriyakale oyambirira a mpingo, kapena aliyense wa Myuda wa Orthodox, ndipo sanazindikire konse kanthu koma Baibulo ili limene ife tiri nalo lero.

⁸⁹ Tsopano, ndiye, mmenemo, mvetserani mwatcheru tsopano. Tsopano inu mukuganiza kuti Akatolika akulandira chikwapu? Mphindi chabe, onani.

⁹⁰ Tsopano, ndiye iwo anapanga bungwe mpingo wa Katolika, ndipo iwo anayamba kuzunza, kuti iwo akana. . .Iwe umachita kumupanga aliyense, kulikonse, mpingo ndi boma, kugwirizana limodzi, ndipo anabweretsedwamo kuchokera ku Roma wachikunja kupita ku Roma waupapa. Mwa kuyankhula kwina, kuchokera ku zamatsenga zachikunja, iwo anatengerapo Chikhristu mu mawonekedwe awo awo. Mwaona? Iwo sakanakhoza kumvetsa chifukwa chimene munthu angaime ndi kupemphera kwa chinthu chosakhalapo. Iwo anali achikunja, kotero iwo anangogwetsera pansi Venus ndi kuimikapo Maria; iwo anagwetsera pansi Jupiter, kuimikapo Petro; mtundu wina wa choimikidwa kuti azichipembedza. Tsopano, ndipo iwo ankapembedza pamaso pa icho. Ndipo iwo anapanga pemphero la konsekonse, kumalinena ilo mu Chilatini kotero kuti izo zisalephereke konse, ndi zina zitero, iwo nthawizonse amanena zofanana.

⁹¹ Ndipo iwe sungakhoze kukambirana kapena kutsutsana ndi wansembe wa Chikatolika, kapena osati wa Chikatolika, pa chikhazikitso cha Baibulo.

⁹² Wina anakhala, wansembe wamng'ono uyu kuno, anali mu nyumba yanga posakhalitsapa. Iye anati, "Inu Aprotestanti, inu mumawerenga Baibulo ndi kukhala kunyumba. Ife Akatolika timapita ku tchalitchi ndi kukapembedza."

Ine ndinati, "Koma chiyani? Ndi chimenecho. Tsopano ndiyankhe ine limenelo."

Iye anati, "Mulungu ali mu mpingo Wake."

⁹³ Ine ndinati, "Iye. . .Palibe chidutswa chimodzi cha Lemba chimanena choncho." Ine ndinati, "Mulungu ali mu Mawu Ake. Iye anati, 'Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga owona.'"

⁹⁴ Iye anati, "Kodi inu simukuganiza kuti gulu lonse la amuna, likukambirana limodzi, lingakhale ndi ulamuliro wochuluka kuposa munthu mmodzi yekha?"

⁹⁵ Ine ndinati, "Ayi. Ngati munthu mmodziyo ali mu chifuniro cha Mulungu, iye ali nacho Choonadi." Nthawizonse zatsimikizira icho.

⁹⁶ Monga ndi Yehosafati ndi Mikaya, maphunziro amene ife tinakhala nawo kumene tsiku lina, Lamlungu latha, pamene Mikaya anapita uko. Ndipo alaliki mazana anai ataima, akunena, "Pitani uko! Ambuye ali ndi inu. Pitani uko! Ambuye ali ndi inu."

Yehosafati anati, "Kodi palibe mmodzi wina kuno?"

Iye anati, "Alipo Mikaya, koma ine ndimamuda iye."

Anati, "Tiyeni ife timve chimene iye atanene."

Anati, “Pitani uko, koma ine ndinaona Israeli atabalalika ngati nkhosa.”

Anati, “Kodi ine sindinakuuze iwe?” Mwaona?

⁹⁷ Kotero, ndani yemwe amalondola, kumeneko? Pamene aneneri mazana anai ophunzitsidwa ataima pamaso pa munthuyo, ndipo komabe woyera-wodzigudubuza mmodzi wamng’ono wakale wamasanza ataima kumbuyo uko anali ndi choonadi. Ndiko kulondola. Ndizo zooni. Iye anachita. Iye anali ndi choonadi. Iye anabwanyulidwa pakamwa kumenyedwa, pa icho, koma iye anali ndi choonadi.

⁹⁸ Kotero izo ziribe kanthu kuti ndi angati amene akunena *izi*, kapena ndi angati akunena *izo*, ndicho chiri PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndizo zooni. Iwe udzayenera kuima pa iwewekha, nthawi zambiri, pamene iwe uyima pa Mawu a Mulungu, koma khala wotsimikiza kuyima ndi chimene Ambuye anena.

⁹⁹ Tsopano, iwo anapanga bungwe mpingo uwu, thupi lalikulu, mpingo wa Katolika, umene uli wolamulira pa zipembedzo zonse, lero, mu malo a Chikhristu, ndi Chikatolika. Koma iwo amati, “Iwe susowa . . . Ise sititero . . .”

¹⁰⁰ Inu mumati, “Inu mumazipeza kuti ‘za kusadya nyama’? Mumazipeza kuti ‘wansembe asakwatire’? Inu mumazipeza kuti *izi*?”

¹⁰¹ Anati, “Ife sitimaphunzitsa Baibulo.” [M’bale Branham agogoda pa guwa nthawi zingapo—Mkonzi.] Anati, “Mpingo ndilo liwu. Ziribe kanthu chimene Baibulo linena; ndi chimene mpingo unena.”

¹⁰² Koma Mulungu anati, “Mulole Mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona.” [M’bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Tsopano iwe uyenera kutenga kusankha kwako.

¹⁰³ Tsopano, Chinikolai icho chinali chitakhala chiphunzitso, ndiyeno chinadzakhala chozunza. Tsopano, pano icho chikutulukira kuno mu masiku otsiriza. Ndiye apo panabwera chitsime, kupyola mu mibadwo ya mdima ndi kuzunza; ndiye apo panadza kulekerera, pa kukonzanso koyamba, kumene kunali Marteni Lutera. Marteni Lutera anatsutsana nawo mpingo wa Katolika, chifukwa cha icho iye anayenda pamenepo ndipo anatenga mgonero umenewo . . .

Ndipo iwo anati, “Ili ndi thupi la Khristu.”

¹⁰⁴ Iye anati, “Ilo si thupi la Khristu. Ndi kokulumunya. Ndicho chonse chimene chiri.”

¹⁰⁵ Iwo amakhulupirira kuti ndi ukalisitiya woyera, umene, “*Ukarisitiya woyera* umatanthauza ‘Mzimu Woyera.’ Ndipo pamene iwe utenga umenewo, iwe umatengera Mzimu Woyera kuulowetsa mu thupi lako.” Ndipo ndiko kulakwitsa.

Mzimu Woyera ndi ubatizo wa Mzimu.

¹⁰⁶ Osati, “Pamene Tsiku la Pentekoste linadza kwathunthu, wansembe anafika ndi kuwapatsa iwo ukarisitiya woyera, kokulumunya pa lirime lawo.” Kapena osati, “Mlaliki wina anawuka ndi kukonkha madzi ena pa iwo, ndi kugwedeza dzanja lawo,” ngakhale. Ayi, bwana.

¹⁰⁷ “Koma apo panadza mkokomo wochokera kumwamba ngati mphepo yamphamvu, imene inadzaza nyumba yonse mmene iwo anali kukhala.” Ndilo Lemba. Ndicho chimene chiri cholondola. Ndicho chimene chinachitika mu Mpingo umenewo, ndipo ndicho chimene chinachitika pamene Kuwala kukuunikila mu tsiku ili. Apo ndi pamene Kuwala kunatulukira kumeneko; ndipo apa ndi pamene Kuwala kukutulukira kuno.

¹⁰⁸ Tsopano ngati Malemba aliwonse, ine ndikuwabwereza, afunsidwa, ingoikani iwo. . . Ine ndikupatsani inu malo amene iwo ali, onani, mu Lemba. Chabwino. Zoono, mu nthawi pang’ono chabe monga iyi. . . Kawirikawiri, pamene ife tipesa Ilo, ife timatenga masabata ndi miyezi. Basi Lemba lililonse, kulitsatira ilo mmusi, kukhala nawo anthu ndi Baibulo lawo. Koma, ngati izo zifunsidwa, mungondilola ine ndidziwe. Chabwino.

¹⁰⁹ Ndiye, Marteni Lutera. Ndiye, atachoka Marteni Lutera, panadza Joni Wesile.

¹¹⁰ Marteni Lutera anatuluka ndi makatekizimu, gawo lalikulu la zinthu. Iye anatuluka ndi ubatizo, iye anatuluka akupereka utatu, ubatizo wautatu umene sunaphunzitsidwe konse mu Baibulo, sunaphunzitsidwe konse mu Baibulo. Kunalibe konse aliyense amene anabatizidwapo mu ubatizo wautatu, mu Baibulo. Ngati ziri chomwecho, bwerani mudzandiwonetse ine pamene izo ziri. Izo siziri mmenemo.

¹¹¹ Njira yokha imene iwo anatumidwa kuti azibatizidwira, inali, “Pitani ndipo mukaphunzitse mafuko onse,” Iye ananena kumbuyo uko, “ndi kuwabatiza iwo mu Dzina,” Osati mu dzina, “mu Dzina; Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ndipo ophunzira anatembenuka mozungulira kumene ndipo anakabatiza aliyense mu Dzina la “Yesu Khristu,” ndi, kulamulira kuti ngati aliyense anakhala atabatizidwapo mwa njira yina iliyonse, amayenera kubwera ndi kudzabatizidwa kachiwiri iwo asanalandire Mzimu Woyera. Ndipo apa panatuluka mpingo wa Katolika. . .

¹¹² Ikani malo amodzi pa Baibulo pamene munthu aliyense anabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ndizo zomveka ndithu, sichoncho izo? Loweruka usiku ndi usiku wa funso, ine ndidzatenga izo, ife tidzatenga kuti tiwongole zimenezo. Chabwino. Chabwino. Ine ndikufuna aliyense amene angakhoze kundiwonetsa ine malo amodzi amene munthu aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ine ndiyenda kuchoka paguwa ndi kunena

kuti ine ndine wachinyengo. Aliyense anabatizidwapo njira ina iliyonse, amayenera kubwera ndi kudzabatizidwa kachiwiri mu Dzina la “Yesu Khristu,” kuti alandire Mzimu Woyera. Ndizo chimodzimidzi. Ndicho chimene Baibulo linanena.

113 Tsopano, inu mukuona, ife timatenga zoganizira mmalo mwa Choonadi. Tsopano inu muyang’ane pa Lemba. Musati munene, kuti, “Chabwino, M’bale Branham anatero.” Inu muyang’ane pa Lemba tsopano. Tengani ndondomeko zanu ndi kuyang’ana pa izo. Ndiyeno mwamsanga. . .

114 Inu mukuzindikira, wina uliwonse wa mibadwo ya mpingo iyo unali ndi Dzina Lake, mpaka iwo utabwera kupyola mu m’badwo wa mpingo wa mdima uwu.

115 Ndipo, penyani, izo kufanizira kumbuyo kutali mu—mu mpingo wa Orthodox. Pamene m’badwo wa mdima kwambiri unkachitika, wa Ayuda, wa Ayuda, unali pamene Ahabu, mu kupambana pambuyo—pambuyo pa mfumu yayikulu ya patsogolo pa iye; ndi patsogolo pa izo, anatengera Israeli yense mu chikhalidwe chokongola. Ndipo Ahabu anabweramo ngati wokhulupirira wammalire, chikhalidwe chofunda, ndipo anapita uko ndipo anakakwatira kalonga wamkazi wamng’ono uyu, Yezebeli, yemwe anali wopembedza mafano, ndipo anamubweretsa iye umo, ndipo anabweretsa kupembedza mafano kulowa mu Israeli. Kodi inu simukukumbukira zimenezo? Choyimira chokongola kwambiri.

116 Pamene Chiprotestanti chinakwatiwa mu Chiroma, iwo anabweretsa kupembedza mafano kachiwiri mu Chikhristu, mu m’badwo wa mdima; chimodzi—chimodzimidzi, mwachirengedwe.

117 Tsopano penyani pamene izo zikufika pa mbali iyi. Kuno inu muli ndi chiyani? Choloweza mmalo cha Mzimu Woyera; kokulumunya. Choloweza mmalo cha ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu Khristu; Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Iwo analoweza mmalo chirichonse. Ine ndikhoza kutenga ndi kutsimikizira mwa Lemba; choloweza mmalo pambuyo pa choloweza mmalo.

118 Ndipo Marteni Lutera anagwirizana nazo izo. Joni Wesile anadza motsatira kumene ndi chinthu chomwecho, ndipo anagwirizana nacho icho. Apo panalibe konse aliyense, mu Baibulo, anakonkha konse. Panalibe konse chinthu choterocho. Panalibe konse chinthu choterocho mu Baibulo, palibe kutuma kapena dongosolo la icho nkomwe, koma inu mumaloleza izo. Ndiko kulondola. Inu mumaloleza izo. Iwo amatuluka ndi kutenga chomwazira mchere chaching’ono ichi ndi kukonkhera iwo pa inu. Chifukwa chiyani? Mpingo wa Katolika unayambitsa izo, ndipo inu mumaweramira kwa izo. Kulondola.

119 Mnyamata anati, tsiku lina, anati, “Inu simuli. . . Inu, inu basi simuli—Mkatolika. Inu muli. . .”

¹²⁰ Ine ndinati, “Ayi, m’bale. Ine ndine Mprotestanti. Ine ndimatsutsa chinthucho.” Ndiko kulondola. Ngati mtumiki wa Uthenga, ndi ana a Mulungu ngati ophunzira anga pano, a Kumwamba, ndipo ine ndiri woti ndiziwalalikira iwo ndi kukhala patsogolo pawo ngati mphunzitsi ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ine ndingakhale wachinyengo ngati ine sindikanamaimira chimene chinali choona. Ine ndinati, “Inde, bwana. Ine ndidzaima, ngati icho chindipha ine. Ine ndipita ku. Ine—ine ndingophunzitsa chimene chiri Baibulo.”

¹²¹ Ndipo ine ndikulolera, pa nthawi iliyonse, kukambirana za Iwo ndi aliyeense, onani; kaya akhale papa wa ku Roma, kapena alikibishopu, kapena chirichonse chimene iye ali. Mwaona? Inde, bwana. Ndiko kulondola. Ngati ine ndikulakwitsa, bwerani mudzandiwonetse ine. Tsopano, ine sindikulakwitsa, chifukwa ine ndikubwereza Lemba. Inu... Ine sinditenga bukhu lanu lowerengalo. Ili ndi Bukhu lowerenga, pomwe pano. [M’bale Branham agogoda kanai—Mkonzi.]

¹²² Tsopano, ndiye, inu mukuzindikira, iwo anayamba kutuluka ndi mawonekedwe onse awa.

Tsopano, mu masiku otsiriza, pali kubwera kuzunza.

¹²³ Tsopano ife tiri, pafupi, Chivumbulutso mutu wa 13 tsopano, kuti tiyambe nawo. Tsopano ngati inu muti muzindikire, mpaka pansu mu mutu uwu pano, anati, “Ine ndinayang’ana, ndipo taonani, Mwanawankhosa anaima pa phiri la Sinai...” Ayi, ine ndikupempha kukhululuka kwanu, ine ndiri mu ndime yolakwika, mutu wolakwika, wa 14. Mutu wa 13:

...ndinaimirira pa mchenga wa mnyanja, ndipo ndinaona chirombo chirinkutuluka kuchokera mu nyanja, chiri nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, ndi pa nyanga nduwira khumi zachifumu, ndi pa—pa mitu pache dzina la mwano.

¹²⁴ Kodi mwano ndi chiyani? Ndi “kuchiseka, kuchinyoza, kuchinena icho.” Tsopano penyani, iye anali ndi “mitu isanu ndi iwiri, nyanga khumi.” Ndipo penyani pamene iye “anabwera kuchokera mu nyanja.” Tsopano Chivumbulutso 17, inu amena mukulemba izo, 17:15, ananena kuti—kuti *madzi akuyimira* “khamu ndi unyinji wa anthu.” Kotero *chirombo ichi chikuyimira* “mphamvu, mphamvu zopanda umulungu.” “Chirombo cholusa chinauka kuchokera mwa anthu, ndipo iye anaima pa mchenga wa mnyanja. Ndipo ine ndinaona chirombo...”

Ndipo chirombo chimene ine ndinachiwonacho chinali ngati... nyalugwe, ...mapazi ake anali mapazi a chimbalangondo, ...kamwa yache...kamwa ya mkango: ndipo chinjoka chinamupatsa iye mphamvu yache, ndi...mpando, ndi ulamuliro waukuru.

125 “Chinjoka!” Ife tiri ndi zinthu ziwiri zoti tizilingalire tsopano. Penyani chirombo ichi. Icho chinali nawo makhalidwe anai osiyana mwa icho.

126 Ndipo ngati inu mutatenga Daniele 7, inu amene mukulemba izo, Daniele 7. Daniele anawona masomphenya omwewo, zaka mazana asanu ndi atatu izi zisanachitike, anawona masomphenya. Iye anawona zirombo izo, zosiyana, chimodzi kwa chimzache, mu kuyamba kwa kulamulira kwa Amitundu.

127 Ndipo pano iwo ali, Yohane akuwona izo, ndi mapeto a kulamulira kwa Amitundu, zonse zinai za zirombo zimenezo zikuimiridwa mu chimodzi. Adierekezi akale omwewo, ziwanda zimene zinagwira ufumu uliwonse wa Aroma, mpaka kupyola, ndi Agriki, ndi ena otero, mpakabe kupyola nyengo ya Amitundu, zabwera mpaka pansu ndipo zonse kukomana mu chirobomo chimodzi. Ife timupeza iye, molunjika, ndi kuwona yemwe iye ali. Kulondola. Zonse izo, nyalugwe, mkango, zonse izo chinjoka. Ndi angati amene akudziwa chimene chinjoka chiri? *Chinjoka* chimaimira “Roma.” Eya.

128 Lolani—tiyeni tiwerenge izo. Izo, izo zakhala ngati zafunsidwa mu malingaliro anu. Ndipatseni ine Chivumbulutso mutu wa 12, mphindi chabe pano. Tiyeni tiwone pano, Chivumbulutso 12. Tsopano penyani.

Ndipo apo panawonekera chodabwitsa chachikulu kumwamba; mkazi. . .

129 Kodi *mkazi* amaimira chiyani? “Mpingo.” Uyu ndi—uyu ndi mkwatibwi apa. Uwu ndi mpingo, mpingo weniweni.

. . . mkazi wovekedwa ndi dzuwa, ndi mwezi pansu pa mapazi ake, . . .

130 Penyani, mwezi pansu pa lake. . . “Dzuwa pa mutu wake, mwezi pansu pa mapazi ake.” *Dzuwa* linali “nyengo ya chisomo.” Ndipo *mwezi* unali “nyengo ya lamulo.” *Mkazi* anali “mpingo wa Orthodox,” ndipo iye anali kuima pa lamulo. Lamulo linali kutsirizika, chifukwa lamulo linali mthunzi wa zinthu zabwino zakudza. Ndi kulondola uko? Mwezi uli kokha mthunzi, wa dzuwa kunyezimiritsa pa mwezi (ndi kulondola uko?), kupanga mwezi. Ndipo lamulo linali pansu pa phazi lake; iye anali atakhala kale moyo kupyola tsiku limenelo. Ndipo zindikirani momwe iye anavekedwera apa tsopano.

. . . ndi pansu pa mapazi ake, ndi pa mutu pake nduwira ya nyenyezi khumi ndi ziwiri: (Mpingo wovekedwa nduwira ndi Chiphunzitsa cha atumwi khumi ndi awiri, mwaona.)

Ndipo iye pokhala ndi mwana analira, kumva kuwawa mu kubala, . . . kupweteka kuti abale. (Uwo unali mpingo wa Orthodox. Penyani.)

Ndipo—ndipo apo panawoneka chodabwitsa china mmwamba; ndipo taonani, chinjoka chofira chachikuru, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri, . . . (onani, sungani seveni ameneyo mu malingaliro anu tsopano, “mitu isanu ndi iwiri,” nthawizonse) . . . mitu isanu ndi iwiri . . . nyanga khumi, ndi nduwira zisanu ndi ziwiri pa mitu yake.

Tsopano, ndipo mchira wache unaguza gawo lachitatu la nyenyezi zammwamba, ndi kuziponyera izo ku dziko lapansi: ndipo chinjoka chinaima pamaso pa mkazi amene anali wokonzeka kuti abale, kuti amulikhwire mwana wake mwamsanga pamene iye ati angobadwa. (Penyani!)

Ndipo iye anabala mwana wamwamuna, amene anali woti alamulire mitundu yonse ndi ndodo yachitsulo: ndipo mwanayo anatengedwera kwa Mulungu, ndi ku mpandowachifumu wake.

¹³¹ Mpingo wa Orthodox utaima pamenepo; dzuwa likuwalira pansu; Chiphunzitsa cha atumwi khumi ndi awiri. Chabwino. Ndi mwezi pansu pa mapazi ake, lamulo, mthunzi wa zinthu zakudza; Kuwala kwa Uthenga kukuwala tsopano, lamulo linazirara pamene Dzuwa linatuluka.

¹³² “Iye anamva kuwawa kuti abale, ndipo iye anabala Mwana Wamwamuna,” amene anali Khristu Yesu, “ndipo Iye anatengedwera kwa Mulungu. Koma mwamsanga . . .” Apa izo ziri. “Mwamsanga pamene chinjoka, chimene chinali Mdierekezi, chinamuwona mkaziyo atakonzeka kuti abale, iye anaima kumene pa iye kuti amulikhwire Mwana Wake mwamsanga Iye akabadwa.”

¹³³ Ndipo pamene Yesu anabadwa, Mfumu ya Roma inapereka kulengeza, kuti aphe ana onse kuchokera usinkhu wa zaka ziwiri, kutsika, kuti afike pomupha Khristu Yesu. Ndipo Mulungu anakokera ubweya pa maso ake, ndi kumutengera Iye uko mu Igupto ndi kukamubisa Iye, monga Iye anachita ndi Mose mwa njira yomweyo.

¹³⁴ Apo pali chinjoka chofiiracho, Mdierekezi. Kodi mpando wake uli kuti? mu . . . Osati mu Russia; mu Roma! Ndipo anati, “Mdierekezi anamupatsa iye mpando wake ndi ulamuliro wake, chinjoka chofiira,” osati Russia.

¹³⁵ Ine ndimamva atumiki aakulu akunena, “Chirasha ndi chotsutsakhristu.”

¹³⁶ Bwanji, Achirasha alibe kanthu kochita ndi wotsutsakhristu. Ndicho chikominsi. Chonyengezera cha Chiprotestanti ndi Chikatolika chabala chikominsi. Chifukwa chimene Russia wawathamangitsira iwo kunja uko, chifukwa iwo anali ndi ndalama zonse. Ndipo anali ndi mapemphero onse atanenedwera kwa oyera amenewo, kotero iwo anamanga

nyumba zazikulu, ndipo anali ndi chuma chonse cha anthu, ndi kuchimanga mtolo icho monga choncho. Ndipo iwo anawona kuti iwo amakhala moyo wosasiyana, ndipo sanali osiyana ndi aliyense wa dziko lonse, ndipo iwo anazilavula izo ndipo anapanga chikominisi.

¹³⁷ Tsopano ngati inu muti mundipatse ine usiku wina umodzi, ngati Mulungu atero, ine nditsimikizira kwa inu kuti chikominisi chikugwira ntchito molunjika mmanja a Mulungu Wamphamvuzonse, kuti awononge Chiroma ci-... Ndipo, kumbukirani, ine ndikunena izi ngati mneneri wa Mulungu, ufumu wa Russia udzagwetsera bomba la atomiki la mtundu wina pa Mzinda wa Vatikani ndi kuwuwononga iwo mu ora limodzi. PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo Baibulo linanena kuti Mulungu anawatenga amuna a mitima ya nkhanza awo ndi kuwaika iwo mmanja Ake, ndipo iwo anali zida mu manja Ake, “kuti akwaniritse chifuniro Chake,” ndi kubweretsanso kwa iye chimodzimidzi chimene iye anali nacho chikubwerera kwa iye. Ndizo chimodzimidzi. Ndiwo Mawu.

¹³⁸ M'bale, inu simukuzindikira basi momwe zinthu izi ziliri zochenjera! Kumbukirani, Yesu Khristu ananena kuti wotsutsakhristu adzakhala wapafupi kwambiri mpaka iye adzanyenga osankhidwa amene. Anati, “Tsopano musati mulole munthu aliyense akudololeni inu.” Anati, “Musati mukhale ngati osapembedza, kunena pemphero lanu mobwereza bwereza, ‘Tikuoneni Maria, wodala muli inu, wodzaza chisomo, ndipo odala ali...’” Anati, “Musati mukhale ngati osapembedza, ogwiritsa ntchito kubwereza kwachabe.” Iye anati, “Ndipo inu musati mumutche munthu aliyense ‘atate,’ pa dziko lino lapansi, ngakhale, olo...pakuti inu muli naye mmodzi Atate, ndipo ameneyo ali Kumwamba.”

¹³⁹ Koma inu mumatembenuka apo, osasamala zimenezo, inu mumachita izo mulimonse, chifukwa izo nzotchuka. Mdierekezi nthawizonse wakhala nacho chinthu chotchuka. Izo nthawizonse zakhala, kuchokera kuchiyambi, “mawonekedwe a chipembedzo.” Kaini anali ndi chinthu chomwecho. Pano pali mzimu wake ukusunthira kumene muno, kupyolera mwa wotsutsakhristu; ndipo apa pakubwera Abele, mmodzi wophedwayo, aponso. Ndiko kulondola. Zindikirani, ndipo tsopano penyani.

¹⁴⁰ Zirombo zonse izi, kumbuyo uko, zonse zinadzatsirizira mu chirombo chimodzi apa, chimene chinkatchedwa “chinjoka chofiira,” Mdierekezi.

Tsopano tiyeni tiyambe pa ndime 15 ya mutu wa 13.

¹⁴¹ Inu mukuona tsopano kuti *Roma* anali—anali “mpando wa Satana.” Chirombo cha mitu-isanu ndi iwiri chokhala ndi nyanga khumi chinaima pambali pa Mwana, Khristu Mwana, kuti amulikhwire Iye basi mwamsanga Iye akabadwa. Ndi

ndani anachita zimenezo? Herode, Roma; nthawizonse wakhala. Ife tifika mu Daniele, molunjika, ngati ife tiri ndi nthawi yokwanira, ndipo Ambuye akatithandiza ife, ndipo ife tiwona.

¹⁴² Monga kulikonse mu Lemba, kuchokera koyambira kwa Amitundu, mpaka kumbuyo kuchokera ku Genesis, ine ndikhoza kutsimikizira kuti Babeloni anayambira mu Genesis ndipo akuthera mu Chivumbulutso. Anayambira kumbuyo komwe uko ndi Nimrodi, mwana wa mwamuna wa Hamu, kupyolera mu kupembedza mafano, kuti abweretse mafano mkati, kuti azipembedza mafano. Ndipo izo zabwera mpaka uko mopyola, ndipo, zochenjera kwambiri mu masiku otsiriza mpaka izo zikudzitengera dzina la Chikristu, ndipo, zikanali, kupembedza mafano!

¹⁴³ Kodi Paulo Woyera wamkulu, mu Atesalonika Wachiwiri sananene? Tiyeni tingowerenga izo, ife tisanapite patali paliponse. Atesalonika Wachiwiri, mutu wachiwiri, ndi kuwona chimene Paulo ananena apa. Iye anachita kuwona izo mu Mzimu, izo zisanafike nkomwe mu tsiku limene ife tikukhalamo.

¹⁴⁴ Chabwino, mai, momwe tsiku limene ife tikukhalamo, mdima umene ife tikukhalamo, ndipo amuna ndi akazi akusonkhana pafupi pano mu mdima wachikunja ndipo sali ngakhale kuzidziwa konse izo. Bwanji—nzachisoni bwanji! Momwe tsiku limene . . .

¹⁴⁵ Paulo anati, “Tsiku limenelo silingati libwere, mpaka kutadza kugwa kotayika poyamba, ndipo munthu wa tchimo kukhala atawululidwa.” Tsopano penyani, iye akumutcha iye kuti akhala munthu. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Paulo anati, “Iye anali munthu wa tchimo, amene amadzikweza yekha pa zonse pamwamba pa zonse zotchedwa Mulungu, kotero iye amene akupembedzedwa ngati Mulungu.” Munthu, kupembedzedwa ngati Mulungu; munthu amene akanati aikidwe apa ngati choyimira kupembedza. Ndipo iye anati, “Tsiku limenelo silikanakhoza kubwera kupatula poyamba pabwere kaye kugwa kotayika.” Ndi chiyani icho? Chikhalidwe chofunda cha mpingo. Chabwino.

¹⁴⁶ Mvetserani. Ndiroleni ine ndikuwerengereni inu izo, ngati inu mungafune, Atesalonika Wachiwiri. Chabwino. Ine ndikhoza kupeza malo olondola tsopano, kuti ndiyambirepo, kotero ife sitisowa kuti tiziwerenga zochulukira chotero. “Musati mulole munthu akunyengeni inu,” ndime yachitatu, Atesalonika Wachiwiri, mutu wa 2.

Musalole munthu akunyengezeni inu mwa njira iliyonse: pakuti tsiku limenelo silidzafika, kupatula patadza kugwa kotayika poyamba, (M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya tsopano)...ndipo munthu ameneyo, (m-u-n-t-h-u, mmodzi)...munthu wa tchimo akhale ataululidwa, mwana wa chiwonongeko;

(mmalo, mmalo mwa Mwana wa Mulungu), *mwana wa chionongeko*;

Amene akutsutsa (yekha) ndi kudzikweza yekha pamwamba pa zonse zimene zikutchedwa Mulungu, kotero kuti iye akupembedzedwa ngati Mulungu; kuti iye ngati Mulungu akukhala mu kachisi wa Mulungu, kudziwonetsera yekha kuti iye ali Mulungu. (Kulandira zolapa!)

¹⁴⁷ Usati undiuze ine, mzanga wa Katolika! [M'bale Branham agogoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Inu mukunena bwanji kuti inu “simumakhulupirira zina koma kukwatira kumodzi; mpingo wa Katolika umayankhula mu kukwatira kumodzi.” Ngati iwe ulibe amayi, izo ziri bwino. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, pomwe pano mwa abale anga omwe; mkazi wamng'ono wakhala pomwe apa, mayi wakhala pano, ndi bambo, nayenso; ndi mkazi wina pano ali ndi mnyamata wamng'ono uyu. Msungwanayo anakwatiwa ndi mnyamata wa Chiprotestanti; iwo analekana ndipo anatuluka. Kotero ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, msungwanayo amapita kukakwatiwa ndi mnyamata wa Chikatolika; ndipo iye anachita kupita uko ndi kukalipira ndalama zambiri, ndi kubwereranso, ndipo, “Iye sanakwatiwe kwa mnyamata wa Chiprotestanti uyu, kuyamba nkuyamba.” Pano pali Howard, abale anga omwe . . .

¹⁴⁸ Chabwino, pamtunda pomwe apa . . . Ine sinditchula dzinalo. Iye ali—iye ali ndi mwana wamkazi, ndipo mwana wamkaziyo ali pafupi usinkhu wa zaka makumi awiri ndi zisanu ndi chimodzi. Mwamuna wake, iye anamusiya iye mu Milltown, ndipo anathawa ndipo anakakwatiwa ndi mwamuna wa Chikatolika. Ndipo tsopano iwo anati, “Iye ayenera kuchoka tchalitchi.” Kotero iwo anapereka ndalama zochuluka chotero, kuti abwerereko ndipo “anamusintha iye kubwerera ku unamwali kachiwiri,” ndipo anamukwatitsanso iye kwa mwamuna uyu. Zovunda! Kumusintha iye kubwerera ku unamwali? Iye anakwatiwa, pamaso a Mulungu, ndipo akukhala mu chigololo. Ndizo zolondola chimodzimidzi. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE, izonso. Zoono.

¹⁴⁹ Ndi chamanyazi bwanji! “Kupereka ndalama zochuluka chotero mmenemo.” Ndicho chifukwa mipingo yonse yayikulu iyi ndi masukulu zikumangidwa. Ndi momwe ziriri. Dziko lonse . . . Inu simukudziwa zimenezo, kuno mu United States. Inu muyenera kudzanditsata ine kutsidya kwanyanja, kamodzi, ndipo inu mudzapeza. Inde, bwana. Inu mupite kumeneko, m'bale, kumene iwo ali ndi dzanja lapamwamba.

¹⁵⁰ Ine ndikhoza kukubweretserani inu chithunzi, chotsimikiziridwa, M'bale Kopp wajambula kumene icho, ndi kuchitumiza kwa ine, cha mlaliki wa Chiprotestanti, mlaliki wa Mzimu Woyera, atagona pa msewu, atafufuma

pafupi ndithu usinkhu *choncho*, iye ndi mkazi wake, ndi msungwana wamng'ono, anafufuma monga choncho; chifukwa iwo analalikira Yesu Khristu, mphamvu ya chiwukitsiro, ndipo anthu amakhoza kupulumutsidwa ndi kulandira Mzimu Woyera. Iwo anawapha iwo pa msewu, ndipo nkusawalola iwo kuikidwa, ndi kumalavulira pa iwo, kwa masiku pambuyo pa masiku. Ndiko kulondola.

¹⁵¹ Komwe komweko kumene M'bale Osborn anachita kugwiridwira, pansi pa mifuti, kuti awatulutse iwo. Iwo anapita kumeneko, ndipo mmodzi . . .gulu la anembe linadza pamodzi ndipo linamupha mnyamata wamng'ono uyu. Ndipo mkazi wake anali atangokhala kumene ndi mwana. Ndipo iwo anayenda kupyola mu msewu monga choncho, ali ndi—ndi—kuperekezedwa pomutengera iye uko ku manda, kukamuika iye. Ndipo mayi uyu akuyenda, ali ndi mwana, akulira, pambuyo pa mwamuna wake wakufa. Ndipo anthu ankayang'ana kuchokera pa zenera, anthu a mtima-woona, anati, “Ngati umo ndi momwe mpingo wa Katolika umamverera, ife tikuwunyoza iwo.” Ndi kumatsatidwa, ndi zikwi, mu msewuwo. M'bale Osborn anali ndi chitsitsimutso kumeneko, mpaka iwo sakanakhoza kumuchotsa iye mu fukolo. Uko kunali anthu ambiri zedi. Ndizo zolondola chimodzimidzi.

¹⁵² O, ndicho chinyengo! Ine ndikudziwa ndicho chithunzi choipa. Ingokhalanibe phee, abwenzi Achikatolika, ife tifika poti tikhule ku mbali inayo, mu maminiti pang'ono. Chabwino. Zindikirani.

¹⁵³ Tsopano ife tati tifike pansi, zindikirani, patsogolo pang'ono. Ndiroleni ine nditengere izi kwa inu. Mwinamwake ine ndikhoza kukhala nayo nthawi, tikadali ndi maminiti makumi atatu apo. Penyani mwatcheru. Tsopano tiyeni tibwerere mmbuyo, mwerengi aliyense, mumalingaliro anu chabe, kwa miniti, kwa chithunzi cha mmaganizo. Pamene . . .

¹⁵⁴ Wokhulupirira aliyense wa Orthodox pano akudziwa kuti ulamuliro wa Amitundu ukuyamba ndi Mfumu Nebukadinezara. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Wokhulupirira aliyense wa Orthodox amadziwa zimenezo. Ndipo Mfumu Nebukadinezara anali ndi masomphenya, ndipo Daniele anamupatsa iye kutanthauzira. Ndi kulondola uko? [“Ameni.”] Ndipo iwo unali mutu wa golide, umene unali Chibabeloni; wachiwiri unali wa Amedi ndi Aperezi; wotsatira unali ufumu wa Agriki; kenako Ufumu wa Chiroma. Ndipo pa mapeto a Ufumu wa Chiroma, Yesu Khristu anali Mwala umene unadulidwa kuchokera mphiri, popanda manja, umene unagudubuzikira mkati ndipo unaswera pansi fano (ndi kulondola uko?), ndi kuphimba dziko lapansi. [“Ameni.”] Aliyense akudziwa zimenezo. Wokhulupirira aliyense amadziwa zimenezo.

155 Ndipo momwe izo, mu masiku otsiriza, pamene iwo anagawikana mu maufumu ambiri osiyana awa, ndi zina zotero, mpaka ku zala, uko kunali chitsulo ndi dongo. Ndipo izo zikutanthauza kuti, mneneri anati, “Mochuluka monga inu munawona chitsulo ndi dongo sizingasakanizikane limodzi, awanso sadzagwirana wina ndi umzake.” Koma iwo adzasakaniza mbewu zimenezo, kuyesera. . . Mwa kuyankhula kwina, iwo adzakwatira mwa iwo, kuyesera kulera ana awo ndi kuswa, chifukwa champhamvu, monga choncho. Ndipo inu mukudziwa ndicho choonadi. Koma, gwirani, ziri nazo, ndipo inu anthu mumagwera pansi kwa izo, “O,” kunena, “ndi zodabwitsa.”

156 Tamuonani Stevenson uyu, chirichonse chimene dzina lake liri, kuno. Tsopano lake. . . kuno. Kodi dzina lake ndi ndani? Ine ndaiwala basi. . . Mnyamata kuno, amene akubweretsa kukangana konse uku kuno. [Osonkhana anena dzinalo—Mkonzi.] Eya. O, mai!

157 United States uyu wavunda mpaka pakati. Inde, bwana. Ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu nthawi kumene imene. . . Mkazi uyu kuno, mmbuyo mu Chivumbulutso 12, pamene. . . Mwana wake mwamuna anatengedwera kukakhala pa Mpandowachifumu wa Mulungu, ndi, pamene izo zinatero, mkaziyo anathawira ku chipululu, kumene iye anakasamaliridwa kwa masiku chikwi mazana awiri ndi makumi asanu ndi amodzi, mpaka chimodzimodzi tsiku la ku Plymouth Rock, chimodzimodzi, kumene mpingo unadzera mpaka kuno pofuna ufulu wa chipembedzo, ndipo iye anakhazikitsa kuno.

158 Ndipo ife tiwerenga mpaka pansi mu mutu wa 13 wa Chivumbulutso apa, ndi kuyang’ana muno pa ndime ya 15. Ndipo, tsopano, miniti chabe, ine ndikufuna kubwerera izo zisanafike, ndipo ife tikuwona kuno kumene kuti Iye anali kuima kuno champhepete mwa nyanja. Tsopano ngati ine ndingakhoze chabe kupeza malowo, pamene, ndime ya 11.

Ndipo ine ndinawona chirombo china chikutuluka kuchokera pa mtunda; (osati kucho—kuchokera mmadzi). . .

159 “Kuchokera pa mtunda.” Ndiye, khamu ndi unyinjira wa anthu ndi madzi, ndiye uku ndi kumene kunalibe anthu, United States.

. . . ndipo icho chinali ndi nyanga ziwiri ngati mwanawankhosa, . . .

160 “Nyanga ziwiri ngati mwanawankhosa,” osati mwanawankhosa. Ndi chiyani icho? Ndi njati yathu ya Chiamereka. Zedi. Onani, apo iye ali, “nyanga ziwiri ngati mwanawankhosa.” Komano kodi icho chinachita chiyani? Icho chinali ndi ufulu wa chipembedzo, poyamba; icho chinkachita ngati mwanawankhosa, icho chinkayankhula ngati

mwanawankhosa. Koma, kumbukirani, icho sichinakhale konse mbuzi yakale. Iye anali Mwanawankhosa. Dziko ili liri kokha usinkhu wa zaka zana ndi makumi asanu, inu mukudziwa, basi mwanawankhosa.

. . . *ndiyeno icho chinayankhula ngati chinjoka.*

Ndipo icho chinachita mphamvu zonse zimene chirombo choyamba chinali nazo chisanakhalepo icho, (chinjoka chofiira), ndi kupangitsa onse amene anali pa dziko lapansi, amene amakhala pa dziko lapansi, kuti azipembedza. . . chirombo, chimene bala lake la ku imfa linachiritsidwa. (Penyani!)

Ndipo—ndipo icho chimachita zodabwitsa zazikulu, kotero kuti icho chipangitsa moto kubwera pansi kuchokera kumwamba. . . (Bomba la atomiki, ndi haidirojini; ophunzira, fuko laluntha, ndi zina zotero, kuyenga mafuko ndi zinthu izi.)

¹⁶¹ United States uyu adzafika ku nthawi imene mpingo ndi boma zidzalumikizana pamodzi. Ndipo Aprotestanti ndi Akatolika adzaponyera zinthu zawo limodzi, kuti amenyane ndi chikominsi. Ndipo ndicho chimodzimidzi kusewera mu manja a chimene Mulungu ananena pomwe apa.

¹⁶² Ndipo inu Achiprotestanti mutagona kutali, tulo tamkonono, mukuwerenga magazini a nkhani yachikondi mmalo mwa Baibulo lanu! Kunja, kumangoyenda mozungulira kwinakwake, ku phwando la mtundu wina, mmalo mwa msonkhano wa pemphero kwinakwake; kumakangana wina ndi mzake za zinthu zakale zazing'ono za mkhutu zimene ziribe phindu mochuluka *chotero*. [M'bale Branham akhwatichitsa chala chake—Mkonzi.] Inu muyenera kukhala pa maondo anu kwinakwake, ngati inu mukudziwa chimene Muyaya ukutanthauza.

¹⁶³ Zindikirani, pamene, Mfumu Nebukadinezara, mu kuyamba mmbuyo kutali, pamene m'badwo wa Amitundu unali kulowetsedwa mkati. Tiyeni tipenye momwe iwo unabwerera mkati. Ndipo njira yomwe iwo unalowera mkati, inu mudzapeza kuti iwo ukutuluka njira yomweyo. Ife tikudziwa kuti pali kuyamba kwa nthawi ya chisomo kwa Amitundu, ndi mapeto a nthawi. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, "Ameni."—Mkonzi.]

¹⁶⁴ Tsopano penyani, pamene Mfumu Nebukadinezara. . . pamene Daniele anatumidwa kupita kumeneko, mneneri wanzeru, pamene Ayuda onse anakhala ngati anachepetsedwa pansi ndipo anali kugwadira kwa Aroma. . . kapena kwa Ababelonia. Koma uko kunali amuna atatu, anai; atatu (Shadireki, Misheki ndi Abidinego), ndi Daniele, amene analinga mu mtima mwawo kuti atumikire Mulungu. Ndiyeno pamene iwo anamuponya Shadireki, ndi ena otero, mu. . . Ndipo

Daniele anali atakhala mwamuna wamkulu, ndipo pamaso pa Nebukadinezara ndi Belshazar, ndi ena otero. Pamene iye anakhala mwamuna wamkulu, tsopano penyani, Mfumu Nebukadinezara anapanga chifano cha golide ndi kuchiyimika icho kunja mmunda, ndi kunena kuti aliyense akanayenera kuti azigwadira kwa chifano chimenecho.

¹⁶⁵ Kodi inu munayamba mwazindikirapo kusalakwa kwa izo, kwa yemwe chifanocho chinapangidwira? Icho chinali Daniele, fano la munthu. Ndipo kodi iye sanati, “mizimu ya milungu,” achikunja? Ndipo monga ife tiri lero, tiri nayo itatu kapena inayi ya iyo. “Mizimu ya milungu inkakhala mwa iye,” ndipo iwo anapanga fano kwa Daniele. Ndipo iye anati, “Onse amene sagwadira chifano chimenecho, aponyedwa mu ng’anjo ya moto.” Inu mukuzindikira, Daniele wachoka powonekera pa nthawi imeneyo. Mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? “Ndipo aliyense amene akanati asagwadire ku fano limenelo akanati adulidwe mu zidutswa, kapena kuponyedwa mu khola la mikango, kapena kuzotchedwa mu ng’anjo ya moto, kapena chinachake, chilango.”

¹⁶⁶ Umo ndi momwe nyengo ya Amitundu inayambira, ndi mawonekedwe a chikunja a kupembedza kwa chipembedzo, ndi kuzunza kuti awapangitse iwo kugwadira kwa icho. Ndipo Baibulo limaneneratu kuti iwo udzatha mwa njira yomweyo, “Munthu woyera,” Yesu Khristu; fano kwa Iye, kuti azipembedza ilo, ndi zina zotero.

¹⁶⁷ Inu mukukumbukira, mu bukhu la ofera la Foxe, iwo ankaika mtanda patsogolo pawo, ankaika ng’ombe pa mkono uliwonse monga choncho, ndipo nkunena... Ngati inu simunyoza, kunyoza Chiprotestanti, ndi kukhala Mkatolika ndi “kupsyopsyona mtanda uwu.” Iwo amayendetsa ng’ombe imodzi mbali imodzi, ndi yina kumbali, ndiyeno nkuwakoka mowang’amba. Iwo ankawawotcha iwo pa nkhuni. Iwo anachita chirichonse. Ine ndafikako ku mphanga za mu nthaka zakale; ine ndikudziwa chimene ine ndikuchiyankhula. Ndipo, onani, izo, ndiko kulondola. Ndipo iwo ali kumeneko. Ndipo zindikirani momwe iwo anadutsira masiku awo a kufera Marteni Lutera asanafike. Molingana ndi Baibulo, nalonso.

¹⁶⁸ Tsopano zindikirani mwacheru kachiwiri tsopano. Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire chinthu chachikulu. Kodi ufumu wa Chibabeloni uwo unasweka motani? Usiku wina pamene iwo anapita ndipo anakatenga zikho zoyera za Mulungu, ndi kuyamba kumwera vinyo mmenemo; kuyamba kukhala ndi nthawi yayikulu, ndi kutengera gulu lalikulu la akazi kunja uko, akazi apadera, ndipo anali kuvina ndi kudyerera ndi kukhala ndi nthawi yayikulu. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Pa nthawi imeneyo uko kunali kulemba kumene kunabwera pa khoma. “*Mene, Mene, Tekele, Ufarisini.*” Kulondola uko? [“Ameni.”] Ndipo iwo anapita

ndipo anakawatenga Akaldia onse, munthu wawo wophunzira, mamembala ofunda a mpingo, ndipo palibe wa iwo akanakhoza kuwerenga izo. Ndiko kulondola.

¹⁶⁹ Koma iwo anali naye mwamuna kumeneko amene akanakhoza kuwerenga malirime osadziwika, aleluya, akanakhoza kuwathanthauzira iwo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iye akanakhoza kutanthauzira malirime osadziwika. Umo ndi momwe iwo unatulukira.

¹⁷⁰ Umo ndi momwe iwo ukutulukira tsopano, ndi mphamvu ya Mzimu Woyera pa anthu amene adzazidwa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, amene ali nayo mphamvu ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Apo ukupita Mpingo wa Amitundu. Apo pali wotsalira.

¹⁷¹ Umo ndi momwe iwo unabwerera mkati, umu ndi momwe iwo ukutulukira, chimodzimodzi, kugwadira ndi kukakamizira ku chipembedzo cha chikunja-chatheka. Ndipo Mulungu kubweramo mu ora lovuta ndi kulemba mu malirime osadziwika, ndipo munthu nkutanthauzira izo. Iye akanakhoza kutanthauzira. Iye sankadziwa chiyankhulo chimenecho; palibe aliyense ankachidziwa icho. Koma iye anali ndi Mzimu Woyera womwewo, umene unamulola iye kutanthauzira izo, ndi Mzimu Woyera womwewo umene uli mu Mpingo lero.

¹⁷² Inu mumazitcha Iwo “zotentheka.” Ine ndivomera kuti iwo ali nazo zochulukira za izo. Koma, m’bale, pali mmodzi weniweni uko, naponso. Ndiko kulondola, umodzi weniweni uko, nakonso. Mdirekezi amaponyera chonamizira chirichonse chimene iye angakhoze, kumene mu njira, kuti akusokoneze iwe. Ndipo ngati iwe sukuganiza nkomwe za Mulungu koposa kukhala panso ndi kuwerenga Baibulo lako, ndi kupemphera ndi kumufunsa Mulungu, ndiye izo zisonyeza kuti iwe suli wokondweretsedwa kwambiri ndi moyo wako.

¹⁷³ Sunthirani kumene kunja uko ndi kunena, “Mulungu, ine sindikusamala kaya ndi nyambo zingati za khwangwala wokalamba zimene Inu mutaike kunja uko. Ine ndikuwona Baibulo Lanu likunena izo, ndipo ine ndatsimikiza!” Ndiko kulondola. “Inu munalonjeza izo kwa ine, mbewu ya Abrahamu.”

¹⁷⁴ Mulungu anakuitanani inu, inu mudzabwera kwa Iyo; koma ngati inu simuli, ine sindikusamala kaya ndinu wachipembedzo chotani, inu mwapita; ndizo zonse, inu simungakhoze kubwera. Palibe munthu angakhoze, kupatula ngati Iye akuitanani inu. Ndipo Iye sakulolera kuti aliyense atayike, koma ambiri a inu mudzatero chifukwa inu muli osakhudzidwa kwambiri za Iwo.

¹⁷⁵ Ndipo inu mudzapita mozungulira ndi kuwona chinachake chikuwoneka motentheka pang’ono, kamthunzi pang’ono, “Chabwino, Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ananena *zakuti-ndi-zakuti*, ndi zina zotero.” Ndiyeno nkuyenda pozungulira

ndi kuchitira mwano Mzimu Woyera, inu mukudziwa ndizo zolondola, ndipo izo sizidzakhululukidwa konse.

¹⁷⁶ Inu mudzapeza mu maminiti pang'ono chimene chilemba cha Mdierekezi chiri, chimene—chimene chisindikizo cha Mdierekezi chiri, chilemba cha chirombo. “Aliyense amene ayankhula motsutsa Mzimu Woyera, iye sadzakhululukidwa, mu dziko ili, kapena dziko likudza.” Upenyeni mpingo woyamba uwo, chimene iwo anachita. Penyani, za uwu, mpingo wachiwiri! Inu mukhoza kudzisindikizira nokha kunja kwa Ufumu wa Mulungu, ndi kulowa mwa Mdierekezi; kunja kumene kulibe “kukhululukidwa, mu dziko ili, ngakhale ilo likudza.” Moona. Koteru, khalani osamalira, yendani molemekeza. Muzikhala osamalira zimene inu mukuchita, chifukwa inu simukudziwa chimene chiti chidzachitike.

¹⁷⁷ Tsopano, ife tikuona zonse izi tsopano zikuwunjikana pansi. Ine ndiri ndi maminiti makumi awiri. Ine ndikufuna inu mutembenuze ndi ine ku mutu wa 17, Chivumbulutso, kuti titsirize mu mphindi pang'ono chabe. Tsopano ife tigunda msewu wa kwathu. Mvetserani mwatcheru. Werengani ndi ine. Tsegulani Baibulo lanu ndipo konzekerani kuti muwerenge. Ichi chiyenera kusindikiza icho.

¹⁷⁸ Kumbukirani, pali zilembo ziwiri; chimodzi ndi chinyengo, chimodzi chinacho ndi Mzimu Woyera. Chimodzi ndi chilemba cha Mdierekezi.

¹⁷⁹ Kumbukirani, ine ndakhala nditanena izi, kuti mpingo woyambirira wa Katolika... Tsopano, anthu Achikatolika, khalani molemekeza kwa maminiti pang'ono. Mpingo woyambirira wa Katolika unapanga ganizo lawolawo za chinthucho. Iwo anali ndi chiphunzitso chabodza, cha ukarisitiya woyera, wa kutenga kokulumunya mmalo mwa ubatizo wa Mzimu.

¹⁸⁰ Achiprotestanti amatenga kugwirana chanza, kapena kupanga lonjezo; onse a iwo akulakwitsa, malingana ndi Mawu a Mulungu. *Ichi* ndicho choyang'anapo. Iwo anabwera ndipo anabatiza, “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” pamene palibe chidutswa chimodzi cha nthawi imene aliyense anabatizidwapo mwa njira imeneyo; umene uli mwamtheradi ubatizo wachikunja, wa Katolika. Ndipo iwo amavomereza izo, ndi kuti, “Inu Achiprotestanti mumagwadira ku ubatizo wathu.”

Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani inu mumachita izo?”

¹⁸¹ Anati, “Mpingo wa Katolika uli nayo mphamvu yosinthira Lemba lirilonse iwo akufuna kutero.”

Ine ndinati, “Ndilo bodza.”

Iye anati, “Nchifukwa chiyani inu mumagwadira kwa iwo nanga?”

¹⁸² A, ndiye inu mumakhala chete. Osati ine! Ine sindimakhulupirira mwa iwo. Awa ndi Mawu a Mulungu. Ndiko kulondola. Ngati anthu akufuna kuwatsatira, iwo ayenera kumapita okha. Ine ndiri woti ndizina Choonadi. Ndiko kulondola.

¹⁸³ Zindikirani, ndiye iwo anatuluka ndi zina zonse izi, mpingo, kulumikiza akatekizimu ake ndi zinthu zonse izo pamenepo. Ndi mulu wotani wa zonyansa ndi zamkhutu! Ndipo iwo wabala mabilioni a osapembedza ndi zozizira za mawonekedwe. . .

¹⁸⁴ Ndi Mdierekezi, pachiyambi. Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti Baibulo linanena apa, “Dziko lonse linadabwa pa mphamvu ya chirombo ichi; chimene chinalipo, chimene kulibe, komabe chiripo.” Izo zingakhale bwanji, “chinalipo, ndipo kulibe”? Anati, “Dziko lonse linadabwa za icho.”

¹⁸⁵ Pamene Roma wachikunja anakhala Roma waupapa, izo sizinaleke. Kachitidwe ka Chiroma kanaleka; pamene mfumu yatsopano inabweramo, iye anangokhazikitsa dongosolo latsopano. Koma pamene izo zinafika mu Roma wachikunja, kupyolera mu mpingo wa Katolika, kupyolera mu upapa, izo sizinaleke konse. Ngati papa wina amwalira, iwo amayikapo wina; papa wina akafa, iwo amaikapo wina. “Chirombo chimene chinalipo, chimene kulibe, komabe chiripo; chimene kulibe, chimene chidzakhalepo; chimene. . . ndipo chidzapita mpaka ku chiwonongeko.” PAKUTI UKUTERO MZIMU WOYERA, kupyolera mu Lemba.

¹⁸⁶ Tsopano, mvetserani. “Ndipo apo panadza mmodzi. . .” Nonse a inu penyani tsopano, mutu wa 17.

Ndipo apo panadza kwa ine mmodzi wa angelo asanu ndi awiri amene anali ndi mbale zisanu ndi ziwiri, (ndizo mbale zotsiriza, zimene zatsanuliridwa), ndipo anayankhula ndi ine, kunena. . . Bwera kuno; ndipo ine ndidzakuwonetsa. . . iwe chiweruzo cha hule lalikulu limene likukhala pa madzi ambiri:

¹⁸⁷ Penyani Chivumbulutso 12. Ameneyo anali mkazi wa unamwali. Iye anali dona weniweni. Momwe iye anaimira mokongola!

¹⁸⁸ Koma apa pali mmodzi amene akutchedwa hule, “h-u-l-e,” amatanthauza wo-. . . Ndi chiyani chimenecho? Tiyeni tichipange fano ichi. . . kapena kuchifotokoza icho.

¹⁸⁹ Mundikhululukire ine. Ikufika mofulumira kwambiri; ndikuganiza ine ndiri ndi maminiti khumi ndi asanu. Ine ndikhala ora lina ndiye, koteru ingokhalani duu. [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁹⁰ Taonani. Chabwino. Taonani, tiyeni tichifotokoze icho bwino. Iye ndi mkazi wauve. Hule ndi chiyani? Ine ndimadana

nazo kunena mawuwo, koma izo zalembedwa pano mu Baibulo. Ndi mkazi amene amadzitcha kuti ali mkazi wabwino, ndipo nkumachita chigololo ndi amuna ena. Tsopano, ngati mkazi akuimira mpingo, ndiye ndi mpingo umene ukudzitcha kuti uli Wachikhristu, ndi kumachita chigololo ndi zinthu zina. Ndi kulondola uko?

¹⁹¹ “Ndipo iye akukhala pamwamba pa madzi ambiri; khamu ndi unyinji wa anthu.” Werengani... pafupi ndime ya 15 ndipo inu muwona zimenezo, onani. Kapena, ya 17, motsatira pamenepo. Ife tifika ku zimenezo mu miniti. “Mkazi amene akukhala pa madzi ambiri; hule.” Ndi chinthu chotani! Tsopano ngati ife tikanakhala ndi masiku ndi masiku, ine ndikanakhoza kumutenga mkazi ameneyo ndi kumufufuza iye kuchokera kwa Kaini mpaka ku Kudza kwa Ambuye Yesu, ndi kutsimikizira kwa inu kuti iye anali mmodzi woyamba kuwupanga bungwe mpingo. Iye ndi mayi wa zabungwe. Penyani, “Ndipo mkazi amene anakhala pamwamba pamadzi ambiri. Pamwamba, akukhala pamwamba pa madzi ambiri.”

Tsopano ndime ya 2.

... amene (m-a-f-u-m-u) mafumu a dziko lapansi achita naye chiwerewere, ndi okhala a pa dziko lapansi apangidwa kuledzera ndi vinyo wa chiwerewere chake.

¹⁹² Mwa kuyankhula kwina, iye akudzinenera kuti ali mpingo wa Chikhristu; wapamwamba, wokongola. Penyani momwe iye wawekeredwa, mu maminiti pang’ono, ndi ngale ndi golide ndi miyala. Iwo akuti, “Ndi ndani yemwe ali ngati iye?”

¹⁹³ Ndipo iye anali ndi chikho mu dzanja lake, chodzaza ndi “vinyo wa ziwerewere zake,” uve wake, chiphunzitso chake chimene iye anali kupangitsa mafumu, o, basi kuti ukhale ndi pemphero laling’ono ndi “kukupempherera iwe uchoke ku purigatorio,” ndi zinthu zonse izi. Ndi zimenezo. Apo inu muli. Amenewo ndi Mawu a Mulungu amene ine ndikuwerenga. Penyani, “Kotero iye ananditengera ine kutali mu... ” Tsopano tiyeni tiwone, ndipo anapanga vinyo... Ndiyo ndime ya 3 tsopano. Chabwino.

Ndipo iye ananditengera ine kutali mu mzimu kupita mu chipululu: ndipo ine ndinawona mkazi atakhala pa chofiira mtund-... chirombo, ... (“Chofiira,” wolemera, mpingo wolemera kwambiri mu dziko.)

¹⁹⁴ Iwo akufuula apa, “Ndani angakhoze kupanga nkondo ndi iye?” Pali mwamuna mmodzi mu dziko, mwamuna mmodzi yekhayo mu dziko, mwa onse a mdziko, amene ali ndi mphamvu ngati masomphenya a Mfumu Nebukadinezara anali. Zala zakuphazi khumi izo zikuyenderera kulowa mu lirilonse... Msempha uja wa chitsulo cha Chiroma ukuyenderera kulowa mu fuko lirilonse mu dziko. Palibe mwamuna wina ayi mu dziko amene ali ndi choyankhula chimene papa waku Roma ali nacho.

Purezidenti Eisenhower akhoza kuyankhula mu United States, ndipo ndi lamulo; koma alipo mafuko ena amene iye akhoza kuyankhulamo, ndipo si kanthu. Koma utsogoleri wolowezana wa Katolika ukhoza kuyankhula mu Roma, ndipo fuko lililonse lidzafuulira kwa icho. Ndiko kulondola. Apo iye ali. Tsopano ife timuona pamene iye ali, ndi kuwona ngati uyo ali iye kapena ayi, kuwona ngati iye akujambulidwa pano molondola. Chabwino.

. . . *ndipo ine ndinaona mkazi atakhala pa chirombo cha mtundu wofiira, (cholemera), chodzala ndi maina amwano, . . .*

¹⁹⁵ Ubatizo wabodza; chuma chabodza; kuwatsogolera anthu mwakhungu, kumawauza iwo kuti akhoza kungobwera ku mpingo, kudzapanga kuvomereza kwawo, ndi zina zotero, kuchita “Tikuoneni Maria,” kuchita kudzitunduza. Umbuli! Zamkhutu! Ine sindikuona momwe anthu, amaganizo abwino achidziko, akanakhulupirira zinthu zoterozo.

. . . *chokhala ndi mitu isanu ndi iwiri . . .*

¹⁹⁶ Apo inu muli kachiwiri, chiwanda chomwechi chimene chiri konsekonse, chinjoka chofiira, chirombo ndi chirichonse, chiri ndi “mitu isanu ndi iwiri; nyanga khumi.”

¹⁹⁷ “Ndipo mkazi,” mkazi, tsopano, mpingo. Tsopano, *chirombo* ndi “mphamvu” iye anali nayo, mpingo wa Chiroma Katolika, koma mphamvu za Chiroma Katolika, pano ndi mpingo ukuyankhula tsopano.

Ndipo mkaziyo anavekedwa mu chibakuwa, ndi mtundu wofiira, ndipo anakometsedwa ndi golide, ndi miyala ya mtengo wache ndi ngale, ali ndi chikho cha golide m'dzanga lache chodzala ndi zonyansa, ndi uwe wa chiwerewere chake:

¹⁹⁸ Ndi uyo apo; ndipo mpingo ndithu inu mukudziwa. Si choncho? Uyenera kukhala pamenepo; iwo ukujambulidwa. Ingowerengani mpaka pansu ndipo ife tiwona yemwe iye ali.

Ndipo pa mutu wake panalembedwa dzina, CHINSINSI, BABELONI WAMKULU, MAYI WA TIMAHULE, CHONYANSA CHA DZIKO LAPANSI.

¹⁹⁹ Chabwino, Achiprotetanti, apa ndi pamene inu mumafika pofinyidwa. Inu muvomereza kuti iye ndi kahule, koma iye anali “MAYI” (wa chiyani, wa ana aamuna?) “WA TIMAHULE.” Amenewo akanakhala *akazi*. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Iyo ikanakhala *mipingo* ndiye. Ndi kulondola uko? [“Ameni.”] Iye ndi mayi wa mpingo ndiye. Sichoncho iye? [“Ameni.”] Kodi Marteni Lutera anachokera kuti? Chikatolika. Kodi onse awa anafungatiridwa kuti? Chikatolika, kubweretsa chiphunzitso chawo chomwecho, ndipo inu mumagwadira kwa izo.

²⁰⁰ Tsopano, mkazi wa uthakati kwambiri mu Jeffersonville akhoza kubala msungwana wabwino, woona, waunamwali, ndiko kulondola, ndipo iye akhoza kupita molunjika ngati iye akufuna kutero. Ndipo chomwechonso umachita mpingo wa Lutera, wa Methodisti, ndi wa Baptisti, ndi wa Presibateria, ndi ena otero; iwo anapita molunjika kwa kanthawi, pamene oyambitsa awo—awo anali pamenepo akulalikira Uthenga kwa iwo. Koma tsopano iwo amapita ku ziwonetsero, kumadansi, televizioni, kusuta, kuchita china chirichonse, (inu mukudziwa ndizo zoonali!), kukhala kunyumba Lamlungu. Ndi chiyani chimenecho? Chifukwa hule lanu likuchita ngati mayi ake. Ndizo chimodzimidzi. Ndizo chimodzimidzi.

²⁰¹ Tsopano tiyeni tiwone kumene mtunduwo uli. Baibulo linati iye anali “MAYI WA TIMAHULE.” Ndipo aliyense amadziwa kuti uyo anali Roma wachikunja, kapena Mkazi wa Roma waupapa, mpingo wa Katolika. Mu miniti, ine ndikuwonetsani inu, mwamalo kuwuika iwo mu dziko lapansi, chimodzimidzi basi kumene iwo uti uzidzakhala. Kulondola. Kumene iwo uli ndi yemwe iwo uli, Baibulo linanena chomwecho. Osati ine; Baibulo! Ndipo linanena kuti iye anabala mipingo ya ana aakazi ambiri pambuyo pake. Chabwino, tsopano, Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi Alutera, ndi ena otero, inu mukuona kumene inu mukufika, “MAYI WA TIMAHULE.” Iwo anakhala moyo molondola, koma pamene Kuwala kunayamba kuwala. . .

²⁰² Ziri ngati gulu la mphemvu mu nthawi ya chirimwe. Kuyatsa getsi, mu msewu pamene mphemvu ikudya pa chitsononkho chakale kapena chinachake chimzake ngati icho, ndi kuyatsirapo kuwala ndipo muwone izo zikuthamangira pokabisala molimba momwe izo zingathere.

²⁰³ Iwe ukalalikira Uthenga, kapena ubatizo wa Mzimu Woyera, kwa ochuluka a mawonekedwe okalamba awa, opanda umulungu; ndipo muwawone iwo, “Ife sitimakhulupirira ayi mu chinthu choterocho. Ine sindimakhulupirira ayi. . .” Chifukwa chiyani? Inu mukudziwa chimene inu muli, pachiyambi. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola chimodzimidzi.

²⁰⁴ Ine sindikunena kanthu kotsutsa mpingo wanu; m’bale, inu muli nawo anthu mmenemo amene ali ngale. Ine sindikunena kanthu kowatsutsa anthu Achikatolika. Ine ndimawakonda anthu Achikatolika mofanana monga ine ndimawakondera anthu a pa Branham Tabernacle. Izo si inu, mzanga, amene ine ndikuyesera kufuulirapo. Si inuyo, Amethodisti ndi Abaptisti ndi Branham Tabernacle. Si inuyo amene ine ndikufuulirapo. Ndi tchimolimine inu mukumulola Mdierekezi kuliika pa inu! Basi chifukwa inu mumapita ku tchalitchi, inu mukuganiza kuti inu muli opulumutsidwa.

Yesu anati, “Kupatula pamene munthu abadwa mwa madzi ndi Mzimu, iye sadzakhoza konse kulowa mu Ufumu.”

Ndipo pamene inu mulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Izo ndizo zochokera mulunjika pa phewa, m’bale, koma chimene chiri mu phewa molunjika kuchokera mu Baibulo. Yesu sanati konse, “Mwinamwake zizindikiro izi zidzawatsata ena.” Iye’ anati, “Izo zidzawatsata iwo.”

O, iwo anati, “Tsopano, ine ndikukhulupirira izo zinali za atumwi. Ine ndikukhulupirira izo zinali za atumwi. Ine ndikukhulupirira kuti pali kuzungulira kumodzi kokha kwa atumwi, ndipo uko kunali mmbuyo umo mu chiyaambi.”

²⁰⁵ Ndipo phunziro lomwe ife tinali nalo usiku watha, “Iye anali ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja Lake,” ndipo nyenyezi iliyonse inali yoti iperekedwe kwa m’badwo wa mpingo uliwonse zikapereke Kuwala, kulondola; basi mofanana monga uko kuli mtumwi *uko*, kuli mtumwi *uko*, ndi mtumwi *uko*, ndi mtumwi *uko*; “imene inali Mizimu isanu ndi iwiri,” mu kuyamba kwa phunziro lathu, “ataima pamaso pa Mulungu, kuti atumizidwe kunja ku Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo.”

²⁰⁶ O, m’bale, iwe ukhoza kuyenda pozungulira ndi kachiphunzitso kena kakang’ono ka Chibaptisti kapena Chimethodisti, ndi kumapita nako iko; koma inu mukayang’ane pa iko, mwa kupenya kwa Baibulo, kamodzi. Ndiko kulondola. Amen. Ine ndikumverera ngati mwachipembedzo pakali pano. Amen. Inde, bwana. Yang’anani. M’bale, ndi zimenezotu. Ndiko kupera; koma kukwapula kulikonse, iko sikumakupangirani inu ubwino wina . . .

²⁰⁷ Mama, akhala kumbuyo uko, iwo anakonda kundipangitsa ine kumwa mafuta a msasi. Ife tinali ana achikale aang’ono. Ife tinkadya nsima ndi nyemba, tsiku lililonse mu sabata, ndi Lamlungu, nalonso. Mwa njira iliyonse, ine ndinkayenera kumwa mankhwala ochuluka. Loweruka usiku, iwo nthawizonse ankandipanga ine kuti ndimwe mafuta a msasi. Ndipo Loweruka usiku ine ndinkachita kugwira mphuno yanga, monga *chonchi*, ine sindikunena izi chifukwa cha nthabwala. Ine ndinkachita kugwira mphuno zanga, ndipo ine ndikakhoha kuti, “Mama, ine sindingakhoze basi kuzimwa izo. Izo zimandidwalitsa ine kwambiri.”

Iwo ankati, “Ngati iwo sakudwalitsa iwe, iwo sakuchitira iwe ubwino ayi.”

²⁰⁸ Chotero ziri Izi. [M’bale Branham tsopano akusasa Baibulo lawo—Mkonzi.] Kukukondoweza iwe! Iwo amapangitsa zako—ziwalo zako zogaira chakudya kuyamba kugwira bwino ntchito, kotero iwe ukhozadi kugaya Uthenga wamphumphu.

²⁰⁹ Achilutera anabwera motsatira ndi kulungamitsidwa. Bwanji, iwo anali chabe. . . Anapanga bungwe icho chonse mmusimo, “Inde, bwana, ife ndife mpingo!”

²¹⁰ Joni Wesile anawona kuyeretsedwa. Iye anati, “Ine ndikuziwona izo mosiyana.” Ndipo iye anati, “Izo zonse nzabwino, Lutera, koma izi ndizo icho.” Kodi iye anali chiyani? Lutera anali nyenyezi ya m’badwo wake, koma pano pali Wesile. Chabwino.

²¹¹ Tsopano, ndiye, Achilutera onse anabwerera pa shelefu, chifukwa iwo anaiwala...sanati atero...Tsopano, osati onse a...Ine ndikutanthauza mpingo wa Chilutera. Achilutera akadali nawobe anthu abwino, odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Koma tsopano iwo onse anabwerera mmbuyo pa mpingo, pa m’badwo umenewo. Chabwino.

Apa panadza Wesile motsatira. Iye anawatengera iwo kupyola m’badwo wake.

²¹² Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, motsatira panadza...Utatha m’badwo wa Chiwesile, panadza Achipentekoste. Ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, kuyankhula mu malirime.

²¹³ Mai, Achimethodisti, ndi Anazareni, ndi Achiyero, amati, “O, ndi Mdierekezi.” Ndipo inu mukuona chimene inu munachita? Inu munachitira mwano Mzimu Woyera. Ndipo mukuona pamene inu muli lero? Ndiko kulondola. Inu, chimodzimodzi chimene inu mwachita. Zedi, inu munatero. Ndipo inu munalephera kuyenda mu Kuwala.

²¹⁴ Ndipo tsopano inu Achipentekoste mwakhala ofunda kwambiri, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwu, mpaka Mulungu akukulavulani inu kuchoka mkamwa Mwake. Kulondola. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

²¹⁵ Inu mukuti, “Kodi inu mumakhulupirira mu kuyankhula mmalirime?” Inde, bwana. “Kodi inu munayamba mwayankhulapo mmalirime?” Inde, bwana. Ine ndikuyamika Mulungu chifukwa cha icho. Inde, bwana. Ine ndayankhulapo mmalirime, nthawi zingapo. Ndipo ine ndikukhulupirira ndi Mphamvu ya Mulungu. Inde. Ine sindimakhulupirira mu umboni weniweni, tsopano, kuti ndi kuyankhula mmalirime. Koma ine ndimakhulupirira kuti pali Mphamvu ya Mulungu imene imakupangitsa iwe kuyankhula mmalirime, zizindikiro ndi zodabwitsa zoti zitsatire. Inde, bwana.

²¹⁶ Ndiyeno Mdierekezi anaika chowopsyezera khwangwala kumeneko, winawake amene ankaseleula ndi kuchita ngati iwo anali nawo Mzimu Woyera. Ndipo nonse inu a Pilgrim Holiness, ndi Achiyero, ndi Anazareni, ndi nonse a inu, munayang’ana mmbuyo ndi kunena, “O, ine sindikufuna kalikonse ka Iwo. U!”

²¹⁷ O, chifundo! Ngati inu mukanakhala nawo Mzimu Woyera, kapena gawo la Mulungu pansu mu mtima mwanu, woyeretsedwa monga inu mumayenera kukhala kuti muli, inu mukanaizindikira iyo kuti ili Mphamvu ya Mulungu. Kodi Yesu sananene, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu

mukanandidziwa Inenso”? Zedi. Ngati kuyeretsedwa ndi gawo la Mzimu Woyera umene unakutsukani ndi kukuyeretsani inu; ngati inu muli nawo Iwo, inu mudzazindikira zonse za Iwo pamene Iwo ubwera.

²¹⁸ Dzanja *ili* limazindikira dzanja *ili*. Mutu *uwu* umazindikira phazi *ili*. Ndi gawo la thupi.

²¹⁹ Ndipo Baibulo linanena kuti pali mphatso zauzimu zisanu ndi zinai; aneneri, aphunzitsi, alaliki, ndi ane- . . . zina zotero; ndi—ndi kutanthauzira malirime, kuyankhula mmalirime, machiritso Auzimu. Ilo lidzazindikira chidutswa chirichonse cha Iwo.

²²⁰ O, inu mumazizidwa, “Ine sindikufuna kanthu kochita ndi Iwo.” Fyuu! Kukufunda kuno, sichoncho? Ndizo zoonā. Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Inu munadzipanga bungwe. Mpingo wanu unanena chomwecho, ndipo ndicho chifukwa inu simukanakhoza kuchita zimenezo. [M’bale Branham anagogoda pa guwa kangapo—Mkonzi.]

²²¹ Koma ambiri a inu Achimethodisti munatuluka ndipo munalandira Mzimu Woyera. Ambiri a inu Achibaptisti munatuluka ndipo munalandira Mzimu Woyera. Inde, bwana. Inu, ndipo ambiri a inu Achiyero munatuluka ndipo munalandira Mzimu Woyera. Inde. Chifukwa chiyani? Inu simunkasamala chimene mpingo unkanena. Inu munayenda mu Kuwala. Ameni. Inu simunasamale chimene chinali kuchitika. Inu munkadziwa kuti izo zinali za Ambuye, ndipo inu munangoyenda basi kulowa mwa Iwo.

²²² Msiyeni wokalamba—msiyeni mayi wokalamba akhale kumbuyo uko, mayi wawo wokalamba. Iye akuchita ngati mayi wake mmbuyo uko, kahule. Iye anapanga bungwe. Ndiyo mfundo kumene ya chiyambi cha vuto, pamene mpingo wa Katolika unapanga bungwe. Ndiye mpingo wa Lutera unapanga bungwe pambuyo pa iwo. Kenako mpingo wa Methodisti unapanga bungwe pambuyo pa iwo. Kenako mpingo wa Baptisti unapanga bungwe. Ndipo tsopano kuli mabungwe mazana asanu ndi amodzi ndi makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi limodzi osiyana. Ndipo Achipentekoste anachita chinthu chomwecho!

²²³ Ulemerero! Chavuta ndi chiyani? Mulungu akutsimikizira kuti Iye sali mu bungwe. Iye ali mu Mzimu, Mzimu Woyera. Aleluya! Aleluya! Inde, bwana.

²²⁴ Iye samasamala chimene bungwe lanu liri. Ndi zamkhutu. Izo ndi zolumikizana ndi Chikatolika ndipo zapita mmbuyo mwa iye, ndipo zakhala mwa iye, ndipo inu mukulandira chilemba chomwecho chimene iye ali. Kodi mngelo sanati, “Tulukani mwa iye, anthu Anga, ndipo musakhale ogawana nawo za machimo ake, ndipo ine ndidzakulandirani inu”? “Musakhudze

ayi chinthu chake chosayera, ndipo ine ndidzakulandirani inu,” Mzimu Woyera ukuyankhula.

²²⁵ “Ndipo aliyense amene atenga chilemba cha chirombo, kapena chilembo cha dzina lake.” Ndikukhumba ife tikanakhala ndi nthawi kuti tilowe mu izo; nthawi yanga yatha. Chilembo cha dzina lake ndi chiyani? Chiprotestanti. “Tiyeni ife tipange fano longa icho. Tiyeni ife tipange bungwe. “Mpingo wathu ndi waukulu basi ngati mpingo wa Katolika.” Iwo anatenga zinthu zonse izi. “Iwo anali ndi mipingo yayikulu, ndipo ife tiri kutero, nafenso. Ife tiri ndi ochuluka chomwecho a kalasi ya mzinda, mu mpingo wathu, monga iwo ali nawo mu yawo. “Tiyeni ife tipange fano kwa chirombo.” Ndipo Baibulo linanena chiyani, iye ndi “HULE,” ndipo ndiyo “KAHULE,” kupyolera mu bungwe.

²²⁶ Koma Mpingo wa Mulungu wamoyo uli mfulu. “Iye amene Mwana wamupanga mfulu ndi mfulu ndithu.” Tulukani mwa iye! Dzadzidwani ndi Mzimu wa Mulungu.

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zomwe Baibulo linaneneratu;
Masiku a Amitundu akwanira, ndi zowopsya
zochuluka;
“Bwererani, O omwazika, kwanu.”

Tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha;
Dzadzidwani ndi Mzimu wa Mulungu, nyali
zanu konzani ziwale,
Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chayandikira! Ameni.

²²⁷ Momwe zinthu zikupitira! Iye anati, mu masiku otsiriza, “Musawope ayi, nkhosa zapang’ono. Ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu,” kukhala limodzi mu malo Ammwambamwamba.

²²⁸ Ndipo inu Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, amene mwawaseka a pentekoste . . .

²²⁹ Ndipo, ine ndikuti, Pentekoste akusowa kukwapula kwabwino kwa Uthenga ka kachitidwe-kachikale, chifukwa iwo anapanga bungwe. A Assemblies of God amene apita mu—chachikulu kwambiri cha Pentekoste, alumikizitsa mgwirizano wa mipingo, basi amawonekedwe ndi osayanjanitsika. Ndipo chachabechabe chimene ine ndinachiwonapo Mzimu Woyera ukuchitiridwa, pafupifupi, zinali ndi mlaliki wa Chipentekoste. Koteru musati muganize, chifukwa inu ndinu a mpingo wa Pentekoste, inu mwapulumsidwa.

²³⁰ Iwe umapulumsidwa kokha pamene iwe wabatizidwa moona ndi Mzimu wa Mulungu, mwa Mzimu Woyera, kulumikizana ndi Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake, kumapita ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, kuwutsatira Mzimu umenewo kulikonse kumene Iwo upita. Zizindikiro zinawatsata

aneneri. Zizindikiro zinamutsata Yesu Khristu. Zizindikiro zinawatsata atumwi. Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo,” mpaka Iye atabwereranso.

“Kodi Ilo linanena zimenezo, M’bale Branham?”

²³¹ “Pitani inu ku dziko lonse, ndipo mukalalikire Mphamvu iyi ndi kuwonetsera kwa fuko lililonse.” Ndipo iyo ikusowa magawo awiri pa atatu a iwobe, sanawamve konse Iwo. “Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo.” “Iwo!” “Fuko lililonse!”

²³² Ulemelero! Fyuu! O, mai! Mwinamwake inu muganiza kuti ine ndapenga. M’bale, ine ndikukuuzani inu, ine ndimakonda chipembedzo chabwino cha nthawi yachikale ichi. Inde, bwana, chimakuzika iwe mwa Khristu!

²³³ Tsopano inu mukuona chimene chilemba cha chirombo chiri? Ndicho chilemba cha chinyengo. Ndi munthu yemwe ali . . . amangogoniza, kuti, “Chabwino, ine ndine wa mpingo, ndipo ine ndiri wabwino basi ngati munthu winayo. Kodi ine sindiri wa mpingo uwu?” Ndipo inu mukuzindikira, kumene bungwe la mpingo wanu umene inu mukudalirapo, kumene iwo unachokera? Kodi inu mukuzindikira?

²³⁴ Baibulo linati, “Iye amene apembedza chirombo, akulandira chilemba chake, kapena chilemba cha dzina lake,” tsopano penyani, “mu mphumi kapena mdzanja,” ndicho *chidziwitso* kapena *ntchito*. Izo sizikutanthauza kuti inu muli ndi chidindo chachikulu pa nkhope yanu. Izo sizisowa kukhala zimenezo. Siziri kuyankhula za kunjja. Ziri kuyankhula pa zauzimu.

²³⁵ Ndipo mpenyeni iye ndi kuwona chimene iye amadziwa za Lemba. Mveterani kwa iye ndi kuwona kumene iye akupitako. “Ngati munthu aliyense alibe Chiphunzitso ichi, mulibe Kuwala mwa iye,” Baibulo linati. Mwaona? Mwaona? Penyani kumene iye akupita. Penyani chimene iye akuchita.

²³⁶ Iye akuti, “Chabwino, ine—ine ndine wa. Ndine Mprotestanti. Inde, bwana. Ine—ine ndine wa mpingo wina *uwu*. Inde, bwana.” Ndipo Lamlungu inu muli nawo chabe pafupi ulemu wokwanira kwa ilo kuti mubwere mkatimo kuchokera mu mvula. Iye amapita uko, mmalo mopita ku msonkhano wa pemphero, inu mumatseka msonkhano, ndi kukhala ndi kumawonera televizioni. Iye amapita kunjja kuno ndipo iye amamwa ndi kumapitiriza, ndi kumachita monga onse a mdziko, komabe iye ndi wa mpingo. Kumbukirani, ndicho chilemba cha tchimo.

²³⁷ Tsopano tiyeni tiwerenge patsogolo pang’ono, mwamsanga, ndiyeno ine nditseka. Ife tadutsitsa nthawi. Tiyeni tiwerenge tsopano ndime ya 6.

Ndipo ine ndinawona mkazi tsopano (mpingo) ataledzera ndi magazi a oyera, . . .

238 “Ataledzera ndi magari a oyera.” Inu mukudziwa, Baibulo linati, pamene iye anawonongedwa, kuti wachivundi aliyense amene anafa, pa dziko lapansi, kulakwa kunapezeka mwa mpingo wa Katolika. Chimodzimodzi, pachiyambi.

...ndi magari a ofera a Yesu: ndi... (Yohane akuyankhula tsopano)...ndipo pamene ine ndinamuwona iye, ine ndinadabwa ndi kuzizwa kwakukulu.

239 Yohane anati! Tsopano tiyeni tiyang’ane apa. Yohane anati, “Ine ndinayang’ana pa iye; iye anali wokongola kwambiri, mpingo wokondeka waukulu. Iwo unali ndi gulu lonse la mipingo itabadwa kuchokera mwa iwo, ‘mayi wa timahule.’ Ndipo ine ndinayang’ana kumbuyo kutali, ndipo momwe mkazi uyo...Iye anali kupereka chiphunzitso chabodza icho, kupangitsa mafumu onse ndi amuna opambana kuledzera nazo izo. Ndipo kuno ana ake aakazi akuchita chinthu chomwecho. Koma, ine ndinayang’ana pa iye; iye anali wokongola kwambiri!”

240 Malo amodzi mu Lemba anati, “Ine ndikukhala ngati mfumukazi ndipo ine sindisowa kanthu.” Mwaona?

241 Ndiyeno iye, Yohane, anati, “Ine ndinazizwa ndi iye. Ine ndinayang’ana pa iye, ndipo ndinayang’ana ndi kuzizwa kwakukulu. Ine ndinazizwa ndi iye.”

Ndipo mngelo ananena kwa ine, Kodi iwe unazizwa ndi chiyani? Ine ndikuuza iwe...Ine ndikuuza iwe chinsinsi cha mkazi, ndi...chirombo chimene chikumunyamula iye, chimene chiri nayo...mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi.

242 Tsopano tiyeni tiwone ngati ife tinali kulondola. Ngati ife tapeza Chikatolika molondola, ndiye inu mukudziwa Chiprotestanti chiri kutsatira iwo. Kotero inu muli...Inu, inu muli ndi luntha lokwanira kudziwa zimenezo, onani. Penyani.

Chirombo chimene iwe unachiwona chinalipo,... kulibe; ndipo chiripo...

243 “Chirombo.” Tsopano penyani. Tsopano inu muzindikira apa, ilo linanena kuchuluka kwa mafumu amene anali pamenepo; angati amene anagwa, mmodzi ayenera kubwera.

...ndipo chidzatuluka kuchokera ku phompho lopanda malire,...

244 Osati pa Baibulo! Kuchokera ku gulu la zamatsenga iwo unapangidwa nazo. Kulibe maziko a zimenezo. Kodi inu mumaipeza kuti “purigatorio”? Kodi inu mumazipeza kuti izi za “kusadya-nyama,” ndi “wansembe osakwatira,” ndi zinthu zina zonse izi zimene iwo amachita, “zovomereza”? Kodi inu mumazipeza izo pati? Palibe malo paliponse oti mungazipeze izo. Izo zinachokera ku gehena. Baibulo linanena chomwecho. Izo

zinachokera, chirombo, mphamvu, chiphunzitso chimene icho chinali nacho, “Zinachokera ku phompho lopanda malire.”

. . . ndipo chikupita *mpaka ku chiwonongeko*: . . .

²⁴⁵ Kodi “chiwonongeko” chiri kuti? Gehena. Kupita mobwerera komwe ku malo amene icho chinachokerako.

. . . *ndipo iwo amene akhala pa dziko lapansi adzadabwa, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu. . . kuchokera ku maziko a dziko, pamene iwo anachiwona chirombo chimene chinalipo, . . . kulibe, ndipo komabe chiripo.*

²⁴⁶ Tsopano, mipingo ya Chiprotestanti imati, “Chabwino, izo zingakhale motani, pamene iwo amati, ‘ine ndikukhulupirira Yesu Khristu. Iye ndi Mpulumutsi wanga?’” Mdierekezi amakhulupirira, nayenso, m’bale.

²⁴⁷ Iko kuyenera kukhala kusintha, Kubadwa kwatsopano, kubadwa kachiwiri. Ndipo pamene iwe ubadwa kachiwiri, dzina lako limaikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

²⁴⁸ Inu mukuti, “Ine ndimadabwa kawirikawiri. Chabwino, bwanji, kodi ine sindiri wabwino ngati wina aliyense? Kodi ine sindiri wabwino monga gulu la inu opanda-pake oyera-odzigidubuza? Ine ndinenso wanzeru. Ine ndiri nazo izo mu. . . Ine ndiri nawo madigirii. Ine ndine wochokera ku koleji. Ine ndimachokera ku banja labwino. Makolo anga anali mamembala a mpingo, ndisanabadwe ine. Kodi sindiri ine wabwino monga inu?”

²⁴⁹ Ilo linati, “Dziko lonse,” Achiprotestanti ndi onse, “anadabwa,” onse kupatula iwo amene maina awo analembedwa mu Bukhu.

²⁵⁰ Nchifukwa chiyani mainawo analembedwa? Iwo ali Mbewu ya Abrahamu, “ndipo ali olowa mnyumba malingana ndi lonjezo, osankhidwa maziko a dziko asanaikidwe.” Ndicho chifukwa iwo samadabwa. Zindikirani apa, tsopano penyani chimene iye ananena. Penyani awa ali mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

Ndipo pano pali mtima umene uli ndi nzeru.

²⁵¹ Tsopano ine ndikufuna ndikufunensi inu chinachake. Kodi nzeru ndi imodzi mwa mphatso za Mzimu Woyera? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi kulondola uko? Ndi angati amakhulupirira kuti Baibulo, Akorinto Woyamba 12, amaphunzitsa kuti mphatso ndi zonsezo mu mpingo, ili nzeru, tiyeni tiwone, imodzi ya mphatso? [“Ameni.”] Chabwino, inu munganene bwanji kuti palibe kuyankhula mu malirime ndiye? Inu munganene bwanji kuti palibe kutanthauzira kwa lirime? Inu munganene bwanji kuti kulibe machiritso Auzimu? Za thupi lomwelo. . . Ngati ine ndiri thupi, ndiri ndi dzanja pa mbali *iyi*, ndi dzanja mbali *iyi*, ndi phazi *apo*; inu munganene

bwanji kuti dzanja liri, osati phazi? Kodi inu simunamve zimene Paulo ananena?

²⁵² Tsopano penyani, iye akuyankhula mu masiku otsiriza, molunjika kwa Thupi, anati, “Pano ziri kwa amene ali ndi nzeru.” O, ine ndimakonda izi. O, mai! Pano pali chimene chiti chikugwedezeni inu. Mvetserani kwa ichi. Chabwino. “Pano pali mtima umene uli ndi nzeru.” Ngati mphatso za Mzimu Woyera izo sizinabwere pansu ku m’badwo wonse uwo, nchifukwa chiyani iye anayankhula izi kwa masiku otsiriza ndiye? Ngati sipadzakhala mphatso mu mpingo, mu masiku otsiriza, nchifukwa chiyani iye analondolera izi ku masiku otsiriza ndiye? “Pano ziri kwa amene ali ndi nzeru.”

. . . Mitu isanu ndi iwiri ndiyo mapiri asanu ndi awiri, pamene mkaziyo akhalapo.

²⁵³ Mapiri angati? Ndi mizinda ingati mu dziko, ngakhale, kuti mpingo wakhala pa mapiri asanu ndi awiri? Umodzi wokha. Uli kuti umenewo? Mizinda wa Vatikani mu Roma. Nkulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Baibulo linanena kuti hule loyipa ili limene linapanga dziko lonse kuchita ziwerewere, ndi kubweretsa gulu la ana aakazi aang’ono kudzaphunzitsa chinthu chomwecho iye anachita; iwo sanali oyipa monga iye, koma iwo anali timahule. Anawaphunzitsa iwo chinthu chomwecho. Anati, “Chiyambi cha iwo chidzakhala chiri mkazi,” kapena mpingo, “ukukhala pa mapiri asanu ndi awiri” mu Roma. Ine ndayang’ana konsekonse pa dziko; ndiuzeni ine kumene iwo uli, “mpingo utakhala pa mapiri asanu ndi awiri.” Tsopano ine ndikuwerenga izi kuchokera mu Baibulo.

Ndipo uko kuli mafumu asanu ndi awiri: asanu agwa kale, . . .

²⁵⁴ Tikanati ife titenge mbiriyakale, ndi kupita mmbuyo kumene ndi kuwonetsa izo, kumene mafumu anagwera, mu Roma, chiyambireni cha ufumu wa Chibabeloni.

. . . mmodzi ali (Nero), ndipo wina ndi woti abwere; ndipo . . . iye ayenera kupitiriza kadanga kakafupi (pafupi miyezi isanu ndi umodzi) pamene iye adza.

²⁵⁵ “Ndipo chirombo . . .” Uu! Penyani pa ichi. Tsopano mphamvu itenga malo a chikunja.

Ndipo chirombo chimene chinaliko, ndipo kulibe, ngakhale . . . ndi chachisanu ndi chitatu, (tsopano penyani) ndipo chiri cha chisanu ndi chiwiri, . . .

²⁵⁶ Inu nonse mukudziwa chimene mfumu yoyipa iye anali. Iye an- . . . Iye anawamangirira amayi ake ku mtengoumodzi wa kavalo ndi kuwathamangitsitsa iwo kupyola mu misewu, ndi kuyatsa mzindawo pa moto, ndi kumakayimba pa phiri. Uwo ndi mtundu womwewo wa mzimu umene ukulamulira mpingo

umene wakhala mu malo a chikunja. “Wachisanu ndi chitatu, amene ali wachisanu ndi chiwiri. Ndiyeno iye alipo, ndipo kulibe; ndipo alipo, ndipo kulibe; ndipo alipo, ndipo kulibe,” mpaka pansu.

. . . ndipo akupita mpaka ku chitayiko.

²⁵⁷ Kupitirira mpakana nthawi ya Kudza kwa Ambuye, ndipo iye akuponyedwa mu gehena.

Ndipo nyanga khumi zimene iwe unaziwona ziri mafumu khumi, amene sanalandire mafumu apabe; koma alandira mphamvu ngati mafumu ora limodzi ndi chirombo.

²⁵⁸ O, ngati ife basi tikanakhala nayo. . . “Sanalandire mphamvu apabe.” Iwo si mafumu. Iwo analibe. . . Iwo sangakhoze. Nyangazo zinalibe nduwira. “Iwo alandira mphamvu za mafumu.” Ndi chiyani icho? Olamulira mwankhanza; osati mafumu ovekedwa korona. Olamulira mwankhanza! O, mai!

²⁵⁹ Tsopano, o, pamene ine ndiwerenga izi, nthawizina mtima wanga umadumpha ndi chimwemwe, chabwino, pamene ine ndiganiza za momwe ife tikukhalira kuno mu masiku otsiriza.

Ndipo nyanga khumi zimene iwe unaziwona ziri mafumu khumi, amene sanalandire mafumu apabe; koma alandira mphamvu ngati mafumu ora limodzi ndi chirombo.

Awa ali ndi lingaliro limodzi, ndipo adzapereka mphamvu zawo ndi nyonga kwa chirombo.

Awa adzapanga nkhondo ndi Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawagonjetsa iwo: . . .

²⁶⁰ Apo pakudza Nkhondo ya Arimagedo; kukonzekera Zakachikwi.

. . . pakuti iye ndi Ambuye wa mbuye, ndi Mfumu ya mfumu: . . . (musati mugwedzedwe) . . . ndipo iwo amene ali ndi iye akutchedwa, osankhidwa, . . .

²⁶¹ Osati inu; Iye ali. Inu muli ndi Mzimu Woyera, inu muyenera kufuula chigonjetso. Mulungu anakusankhani inu asanakhalepo maziko a dziko. Ngati inu simungakhoze kuwona Kuwala kwa Uthenga, ndicho chifukwa inu—inu muli chabe akhungu.

. . . osankhidwa, ndi okhulupirika.

Ndipo iye ananena kwa ine, Madzi amene iwe unawawona, kumene akhalako hule, ali anthu, . . . khamu, ndi mafuko, ndi malirime.

²⁶² Mwa kuyankhula kwina, mkazi uyu amene akukhala apa, mpingo, apereka chiphunzitso chake kwa anthu onse, khamu, ndi lirime. Ndi uyo pamenepo. Iye anali ndi ulamuliro pa iwo. Iye akukhala pa iwo, mphamvu kuwalamulira iwo. Iye

akukhala pa mapiri asanu ndi awiri, atavekedwa mu chofiira, wokongoletsedwa molemera kwambiri pa dziko. Ndi uyo apo.

Ndipo nyanga khumi zimene iwe unaziwona pa chirombo, izi zidza...

²⁶³ Penyani tsopano, inu mukubwera mu mphamvu za chikomini.

...awa adzamuda hule, ndipo adzamupanga iye kukhala bwinja ndi wamaliseche, ndipo adzadya thupi lake, ndi kumuwocha iye ndi moto.

Pakuti Mulungu waika mu mitima yawo kuti akwaniritse chifuniro chake, ndi kugwirizana, ndi kupereka ufumu wawo kwa chirombo, mpaka mawu a Mulungu... akhale atakwaniritsidwa.

²⁶⁴ Aleluya! “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu a Mulungu sadzapita konse.” Penyani!

...mkazi amene iwe unamuwona...

...mkazi amene iwe unamuwona ali mzinda waukuluwo, umene umalamulira pa mafumu a dziko lapansi.

²⁶⁵ Ndiwonetseni ine mzinda umodzi mu dziko umene ukulamulira pa mafumu a dziko lapansi, kuchokera ku njira iliyonse imene inu mukufuna, kunja kwa ufumu wolowezana wa Chikatolika mu Roma, wakhala pa mapiri asanu ndi awiri. Palibe mzinda umodzi, ndipo sipanakhale konse, ndipo sudzakhapanso; kunja kwa Mzinda Watsopano umene ukubwera kuchokera Kumwamba. Ndiko kulondola.

²⁶⁶ Tsopano, miniti yokha. Ine ndikufuna ndikusonyezeni inu ichi kachiwiri, kotero Ambuye akhale akukumbukira ndi kutidalitsa ife pamodzi pamene ife tikuwerenga izi. Chabwino. Penyani pano tsopano, ine ndikuwerenga mutu wa 13. Ine ndikuyambira pa ndime ya 15.

Ndipo iye anali ndi mphamvu kuti apereke moyo kwa fano...

²⁶⁷ Ndimu mu United States, pomwe ife tamuona akubwerako, inu mukuona, fano.

...kuti fano la chirombo liyenera nalo kuyankhula, ndi kupangitsa ochuluka amene sangapembedze fano la chirombo kuti apedwe. (Ndicho kuwukira.)

Ndipo iye anapangitsa onse, onse aang’ono ndi aakulu, olemera ndi osauka, wamsinga ndi mfulu, kuti alandire chilemba mu dzanja lawo lamanja, kapena mu kapitawo zawo...-mphumi.

Ndipo kuti pasakhale munthu ati agule kapena kugulitsa, kupatula iye amene anali ndi chilemba,

kapena dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake.

²⁶⁸ Tsopano penyani, tsopano, mwatcheru tsopano, mwatcheru kwenikweni, ife tisanatseke. Ndime ya 18. Mvetserani.

Pano pali nzeru.

²⁶⁹ Mukuona Mzimu Woyera ukuyitananso kwa okhulupirira mu tsiku lotsiriza? Gulu laling'ono ilo uko, likuyankhula, kuitana ku gulu laling'ono mu tsiku ili, "Apa ndi kwa iye amene ali ndi nzeru mu mpingo. Mloleni iye amvetse izi."

...Mloleni iye amene ali nako kumvetisa awerenge chiwerengero cha chirombo: pakuti ndicho chiwerengero cha munthu, (osati fuko) munthu; ndipo chiwerengero chake ndi mazana Asanu ndi limodzi makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu ndi chimodzi.

²⁷⁰ Ndipo ku Mzinda wa Vatikani komweko...Musati mundiuze ine tsopano; Ine ndiri nazo *Zowona Za Chikhulupiro Chathu*, ndi zonse, onani. Uko ku Mzinda wa Vatikani, ndipo papa akuima ngati "wolowa mmalo a Mwana wa Mulungu." Ine ndiri nawo amzanga Achikatolika akhala pomwe pano, amene anali Akatolika, akhala pano ndipo akudziwa kuti ndizo zooni. Makolo anga, mwinamwake, ndisanakhalepo ine, anali Akatolika, nawonso. Mukuona?

²⁷¹ Iwo anamutcha Patreki Woyera Mkatolika, ndipo iye sanakhale konse Mkatolika. Anati Joani waku Arc anali woyera; ndipo ansembe anamuwotcha iye ngati mfiti. Nzosadabwitsa Yesu anati, "Inu mumayeretsa manda a aneneri, ndipo inu munawaika iwo mkati mmenemo, inu mumayeretsa makoma." Ndiko kulondola.

²⁷² Penyani, ndi chiwerengero cha munthu. Ndipo pa papa wa ku Roma, panalembedwa, "VICARIVS FILII DEI." Izo zinalembedwa mu zilembo za Chiroma. Ingolembani izo nokha, mawa. V, I, C, I, R, o, ingosungani izo, mu zilembo za Chiroma, ndipo mujambule mzere wanu ndi kuwonkhetsa, ndipo muwone chimene inu muli nacho: sikisi handiredi ndi sikisite sikisi. Kodi iye akukhala kuti? "Pa mapiri asanu ndi awiri."

²⁷³ Ndipo kuchokera kumeneko kunabwera bungwe la chipembedzo, chimene chinkaphunzitsa mbalume mmalo mwa Baibulo. Ndipo Aprotostanti anatuluka kuchokera mu izo, ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho basi chimene iwo ali, chifukwa Ilo linati iye anali "HULE," ndipo iwo anali "TIMAHULE." Kutulukamo ndi ubatizo wabodza, ndi chipembedzo chabodza, ndi lingaliro labodza la Mzimu Woyera, ndi lingaliro labodza la gehena, ndi zinthu zina zonse izi monga choncho, ndipo Aprotostanti akutsatira mpaka mmusi moponda mapazi.

Koma kudzakhala Kuwala mu nthawi ya
 madzulo,
 Njira ya Ulemerero inu mudzaipezadi; (ndiko
 kulondola)
 . . . njira, ndiko Kuwala lero,
 Kuikidwa mu Dzina lofunika la Yesu.
 Ana ndi aakulu, lapani za tchimo lanu lonse,
 Mzimu Woyera zedi udzalowa mkati;
 Kuwala kwamadzulo kwafika,
 Ndi choona kuti Mulungu ndi Khristu ndi
 mmodzi. (Ameni!)

²⁷⁴ M'bale, ine ndikukuuzani inu, ndi Nyali zamadzulo zimene zikuwala. Chiphunzitsa chomwecho chautumwi, ubatizo womwewo wautumwi, kudzazitsa komweko kwautumwi kwa Mzimu Woyera, zizindikiro ndi zodabwitsa zomwezo zautumwi, zikusuzumira mopyola kwa amitundu; monga izo zinawachitira Ayuda, kumbuyo uko pa mmawa wolawirira, kuno izo ziri mu kulowa kwa dzuwa.

Kuli anthu pafupi kulikonse,
 Amene mitima yawo onse ili pamoto
 Ndi moto umene unagwa pa Pentekoste,
 Umene unawayeretsa ndi kuwatsuka iwo;
 O, ukuyaka tsopano mu mtima mwanga,
 O, ulemerero ku Dzina Lake!
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wa iwo.

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wa iwo;
 Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wa iwo.

Anasonkhana mchipinda chapamwamba,
 Onse akupemphera mu Dzina Lake,
 Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,
 Ndipo Mphamvu ya utumiki inadza;
 Tsopano chimene Iye anawachitira iwo tsiku
 lija
 Iye adzachitira inu chomwecho,
 Ndine wokondwa kwambiri kunena kuti ndine
 mmodzi wa iwo.

Sichoncho inu? [Osonkhana anena, "Ameni."—Mkonzi.]

Bwerani, m'bale wanga, dzafuneni dalitso ili
 Limene lidzayeretse mtima wanu ku tchimo,
 Lidzayambitsa mabelo achimwemwe kulira

Lidzayika moyo wanu pamoto;
 O, likuyaka tsopano mu mtima mwanga,
 O, ulemerero ku Dzina Lake,
 Ndine wokondwa kwambiri kunena kuti ndine
 mmodzi wa iwo.

275 O, chifukwa cha Uthenga wa ulemerero uwu!

Ukuwukha mmagazi, ee, ukuwukha mmagazi,

276 Werengerani mtengo wake! “Ngati iye ati anditsate Ine, msiyeni iye adzikane yekha, atenge mtanda wake (imfa) ndi kunditsata Ine.”

Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi,
 Magazi a ophunzira omwe anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera,
 Anali Yohane Mbatizi, koma iye anafa ngati
 munthu;
 Ndiye anabwera Ambuye Yesu, iwo
 anamupachika Iye,
 Iye analalikira kuti Mzimu udzapulumutsa
 anthu ku tchimo.

Kunali Petro ndi Paulo, ndi Yohane
 waumulungu,
 Anapereka miyoyo yawo kuti Uthenga uwu
 uwale;
 Iwo anasakaniza magazi awo, ndi aneneri
 akale,
 Kuti Mawu owona a Mulungu akhoze
 kunenedwa moona.

Ndiye anamugenda Stefano, analalikira
 motsutsa tchimo,
 Iye anawakwiwitsa iwo, iwo anaphwanyira
 ubongo wake mkati;
 Koma iye anafa mu Mzimu, anapereka mzimu,
 Ndipo anapita kukalumikizana ndi ena,
 khamu lopereka moyo lija.

Ukuwukha magazi, ee, ukuwukha magazi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu umawukhabe
 magazi,
 Magazi a ophunzira omwe anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu unali
 kuwukhabe magazi.

Miyoyo ya pansi pa guwa, ikulira, “Mpaka liti?”

Kuti Ambuye muwalange iwo amene achita cholakwa; (kunyozza, mwaona. O, mai!)

Koma alipo ena ati apereke magari amoyo
Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu
ndi kusefukira kofiira.

Ukuwukha magari, ee, ukuwukha magari,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukhabe
magari,

Magari a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magari.

²⁷⁷ Tiyeni titembenukire pozungulira, gwiranani chanza ndi wina tsopano.

Ukuwukha magari, ee, ukuwukha magari,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magari

Magari a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magari.

²⁷⁸ Kodi inu mukuwakonda Ambuye? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ambuye akudalitseni inu.

²⁷⁹ Atate, ife tikupemphera kuti Inu mudalitse omvera awa, ndipo mulole iwo azipita kwawo akusangalala. Mulole iwo akabwere ku Kasupe wodzaza Magari, otumphuka kuchokera mu misempha ya Emanuele. Mulole iwo asiye za mwachimpingo, ndi kubwera ndi kudzalandira Mzimu Woyera. Ife tikupemphera mu Dzina la Yesu. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu. Usiku wabwino. Mulungu akhale ndi inu.



CHILEMBA CHA CHIROMBO CHA54-0513
(The Mark Of The Beast)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lachinayi usiku, Mei 13, 1954, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1996 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org